


# AHEBRI, MUTU

## WACHISANU NDI CHIWIRI <sup>1</sup>

 ...usiku, ndi kumumva Joyce akuimba. Kodi inu mumadziwa kuti icho ndi chozizwitsa mwa ichochokha? Msungwana wamng'ono uyo, iye angakhoze bwanji kumaganiza izo zonse? Ndipo usiku uliwonse iye ali nayo kwa ife yatsopano. Momwe iye angakhoze kumaganizira zonse izo, awo ndi kwenikweni malingaliro akatswiri. Ambuye amudalitse mwana ameneyo.

<sup>2</sup> Tsopano, mawa, pa hafu pasiti thuu, ku nyumba ya maliro ku Charlestown, Indiana. Mlongo wathu wokondedwa, yemwe wapita, Mlongo Colvin, ife tikumupatsa iye ulemu wotsiriza, k—ku nyumba ya maliro ndi kumanda, mawa madzulo. Mmodzi yemwe anakhalapo moyo monga inu muliri usikuuno, ndipo iye wadutsa kupyola chotchinga komwe inu mudzatero nthawiina. Ndipo onse omwe akufuna kuti akakhale nawo pa mwambowo, bwanji, ali olandiridwa kuti abwere. Ilo ndithudi likakhala thandizo lalikulu kwa banja la a Colvin, kukadziwa kuti kachisiyu kuno, komwe iwo onse akhala akupita ku mpingowu motalika kwambiri, ndi zina zotero, atero. Ife tikhala okondwa kukhala nanu mutabwera uko. Ndipo ine ndikuganiza . . . M'bale wathu wokondedwa McKinney, mmodzi yemwe analalikira pa maliro a m'bale wanga, zaka zambiri zapitazo, akakhala ndi gawo lalikulu la malirowo, ndipo ine ndafunsidwa kuti ndibwere ndi kukamuthandiza iye m—mu mwambo wa maliro.

<sup>3</sup> Tsopano, ine ndinali nditachedwa pang'ono pokha, usikuuno. Ine ndinali ndi zitsulo zambiri mu moto, ine sindimadziwa njira yoti ndipite. Pali kuitana kochuluka, ndi kuphwanyana uku ndi ngozi, ndi anthu akuitana, kubwera. Mpaka, ine ndangochokera kumene ku Lousville, mphindi zingapo zapitazo, kuti ndibwerere kuno mwamsanga, ndipo ndasiya kuitana kungapo zomwe ziri zolemetsa kwenikweni ndipo ziyenera kuti zichitidwe, ine ndikuganiza, komabe, usikuuno. Ndipo tsopano zitipemphererani ife pamene ife tikupitirira nazo.

<sup>4</sup> Ndipo mmawa uno i—ine sindinafike ku wanga—mutu wanga, ku mutu wa 7 wa Bukhu 1—1—la Ahebri. Ndipo pamene ife tikutembenezira kwa iwo, usikuuno, ine ndikufuna kuti ndilengeze za msonkhano wa M'bale Graham Snelling, uko ku hema kumtunda uko, kumapeto kwa Msewu wa Brigham. Ngati Ambuye alola, ine ndikufuna kuti ndidzabwerere Lachitatu usiku. Ndipo kumeneko ife tikonza usiku wina womwe ife

titi tidzapite uko ngati nthumwi, sabata ino nthawiina, kuti tikamuchezere M'bale Graham mu msonkhano. Ndipo iye ali. . . akuti, "Akukhala ndi gulu labwino." N—ndipo iye akatiyamikira ife kubwerako, pa thandizo limeneli. M'bale Graham Snelling, aliyense wa inu wakhala akukhalapo pa msonkhanowo, kapena akufuna atatero, ndi basi kumapeto kwa Msewu wa Brigham kumtunda uko. Aliyense akhoza kukuuzani inu komwe iwo uli. Kumapeto komwe kwa bwalolo, hema waikidwako. Iye akuyamikira chigwirizano chanu. Chifukwa, ife ngati kachisi talonjeza chigwirizano chathu ndi iye, magawo zana pa zana, kotero ife tikuyesera kuti tithandizire.

<sup>5</sup> Tsopano, ndiye posachedwa ife tikufika mpaka pa malo a, Ambuye akalola, ku mutu wa 11 wa Ahebri, mu mausiku pang'ono, ngati Mulungu alola, ndipo apo ine ndikuganiza ife tikakhala ndi nthawi yaikulu naponso.

<sup>6</sup> O, Ambuye anataliditsa ife mmawa uja mwa njira yododometsa, momwe Iye anatsanulira Mzimu Wake pa ife! Ndipo tsopano, usikuuno, ife tikumuyembekezera Iye kuti achita izo mobwerezaz; ndiyeno Lachitatu usiku, ndi kupitirira. N—ndipo mausiku omwe ine nditasowepo, M'bale Neville akhala ali pano kuti azitenge izo mopitiriza, ngati ine ndichokapo.

<sup>7</sup> Ine sindimadziwa konse chomwe ndingati ndichite, iwe ukhoza kukhala pano ora ili, ndipo ora lina nkuitanidwira ku California. Mukuona, iwe sumadziwa basi komwe Ambuye angati akutumize. Ndicho chifukwa kuli kovuta kuti ine ndipange ndondomeko ndi kuti i—ife tichita *chakuti-n-chakuti*. Ine ndikhoza kuyamba kumachita chinthu chinachake, Ambuye nkunditumiza ine kwinakwakenso. Mukuona? Chotero ife sitimadziwa basi zomwe Iye angati achite. "Koma ngati Ambuye alola," ife timatero. Ine ndikuganiza ife timatumidwa, kapena timalamuliridwa zimenezo, mu Baibulo, "Ngati Ambuye alola, ife tichita zinthu *zakuti-n-zakuti*." Kotero ngati ife sitipezeka tikukwanitsa zogwirizana zomwe ife. . .kapena kukwaniritsa zogwirizana, ife timamverera kuti mwina Ambuye sanali kulola kuti izo zichitike.

<sup>8</sup> Tsiku lina, ife tinagwidwa, M'bale Roberson ndi M'bale Woods ndi ineyo. Ndipo ife timadabwa, "Bwanji?" Ine ndinali nditakhala pamenepo tikuyang'ana pa mapu, tikubwera chotsika khomwe, ndipo ife tinayendetsa mailosi 50 mobwerera kumene kumpoto pa msewuwo. Ndipo ine ndakhala ndikuyendetsa pa msewuwawukuluwu kuyambira ine ndiri wausinkhu wa zaka fortini. Ndipo ine ndinadabwa momwe ine ndinachitira konse izo. Ife tinali titaima apo, atatu tonse ife. Ife tonse tayendapo pa misewu yaikulu. Tikuyang'ana kumene pa mapu, kukhalabe pa 130, tikubwera podutsa Illinois, ndipo tinapanga kukhota kwakung'ono chabe, osazindikira kuti dzuwa linali kumbuyo kwathu mmalo mokhala kutsogolo kwathu. Ife tinali tikupita kumpoto mmalo mwa kummwera.

Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, tinawoloka msewu, ine ndinati, “Uwu si msewu wolondola.” Ndinayang’ana pansi apo, ndipo ndinadzapeza kuti, ife tinali mailosi fifite kunja kwa njirayo. Tinapita molunjika ndithu mmbuyo. . . ? . . .

<sup>9</sup> Ndiye pamene ife timabwerera, i—ife tinali kuyankhula. Ine ndinati, “Inu mukudziwa chifukwa chake? Ife. . . Ambuye mwina anatilambalalitsa kuno, kutipewetsa kuti tikanakhala ndi ngozi yowopsya kuno kwinakwake, yomwe ikanakhoza kuchita chinachake mwamtundu wina. Ife tikudziwa kuti zinthu zonse zimachitira ubwino kwa iwo omwe amawakonda Ambuye. Ndi zonse zomwe ife tiyenera kumazisunga mmalingaliro.”

<sup>10</sup> Tsopano, usikuuno, ife tikuyamba tsopano kwa phunziro laling’ono lophunzitsa. Ndipo ngati ndiri. . . ine sindikuganiza kuti tifika mmusi, mwinamwake titero usikuuno, ku. . . Uwu ndi mutu wawukulu wa kuphunzitsa pa kupereka zachikhumi, kwa mpingo. Ndipo ilo ndi phunziro lalikulu, lomwe ife tikhoza kukhala pa ilo kwa masabata ndi masabata, pa chinthu chimodzi icho, momwe Abrahamu anaperekera chakhumi kwa Melkizedeki, ndi ngati izo ziri zofunikira.

<sup>11</sup> Kodi chokupizira mphepo ichi chikumupweteka aliyense kumbuyo uko? Kodi inu mukanafuna icho chitathimitsidwa? Ngati icho chikumupweteka aliyense, kukupizira mu nkhope yawo, chirichonse cha zokupiza mphepozo. Ngati icho chiri, mungokweza manja anu. Ndipo, kapena mungomutumama mmodzi wa othandizira, mtumizeni winawake kwa m’bale pano, iye akuzimitsirani inu icho. Ndipo ine ndimakhala ngati kuchithawa icho mwiniwanga; ine ndimatenthedwa ndipo ine ndimachita thukuta, ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, i—ine ndimasasa mawu. Kotero, icho chiri pa inu, kotero icho sichindivuta ine mwanjira iliyonse. Ife tikufuna kuti inu mukhale motakasuka tsopano.

Ife sitiyesera kuti titenge nthawi yanu yochuluka, koma ife tikuti tingoyang’ana molunjika mu Mawu. Ndipo ife tisanachite izo, tiyeni tiyankhule kwa wolembayo mphindi yokha.

<sup>12</sup> Tsopano, Atate Akumwamba, ife sitikudziwa zomwe mwatisungira. Koma chinthu chokha chimene ife tikuchidziwa, ndipo tiri okakamizidwa, nkuti zinthu zabwino ziri patsogolo pathu. Pakuti kunalembedwa, “Diso silinawonepo, ngakhale khutu silinamvepo, komanso sizinalowepo mu mitima ya anthu, zomwe Mulungu wawasungira iwo, omwe amamukonda Iye.”

<sup>13</sup> Ndipo ife tikupemphera kuti Inu mutsegule mazenera a Kumwamba usikuuno, mu nyumba Yanu yosungiramo, ndi kutipatsa ife Mawu Anu, omwe ati akhale chinachake chomwe chiri choyenera, chinachake choti chichulukitse chikhulupiriro chathu monga Akhristu, ndi kutipanga ife mochuluka—okhazikika mochuluka pa Uthenga, kuposa chomwe ife tinali pamene ife timabwera muno. Perekani izi, Atate. Mulole Mzimu

Woyera utenge Mawu a Mulungu ndi kuwapereka Iwo kwa mtima uliwonse momwe ife tiriri ndi chosowa. Mu Dzina la Yesu ife tikupemphera, Mwana Wanu wokonedwa. Amen.

<sup>14</sup> Tsopano, mmawa uno, posiya ndime yotsiriza ya mutu wa 6, kotero ife tikhoze kupita kumene mu wa 7

*Momwe wotsogolera wa ifeyo analowamo, ngakhale Yesu, atakhala wansembe wamkulu kwa nthawizonse, monga mwa dongosolo la Melkizedeki.*

<sup>15</sup> Tsopano ife tikuti tiwerenge ndime zitanu zoyambirira, kapena ndime ziwiri zoyambirira, kapena ndime zitanu zoyambirira, kani, za mutu wa 7, kuti ife tikhoze kuyamba pomwepo.

*Pakuti Melkizedeki uyu, mfumu ya Salemu, wansembe wa Mulungu Wamkulukulu, amene anakomana ndi Abrahamu akubwerera kuchokera kokapha mafumu aja, ndipo anamdalitsa iye;*

*Kwa yemwenso Abrahamu anampatsa gawo la khumi la zonse, (ndi icho chachikhumi chanu); poyamba pokhala mwa kutanthauzira Mfumu ya chilungamo, . . . pameneponso Mfumu ya Salemu, yomwe ili, Mfumu ya mtendere;*

*Wopanda atate ache, wopanda amache, wopanda fuko lochokerako, . . . ngakhale chiyambi. . . wopanda ngakhale chiyambi cha masiku, ngakhale chitsiriziro cha moyo; koma wopangidwa monga Mwana wa Mulungu; akhala wansembe kosalekeza.*

<sup>16</sup> Neno lodabwitsa lakelo! Tsopano ife tikuyenera kuti tibwerere mu Chipangano Chakale, kuti tikakumbemo zinthu zonona zazikulu izi. Ndipo, o, momwe ine ndikuzikondera izo!

<sup>17</sup> Inu mukudziwa, uko mu Arizona, ife tinkakonda kufufuza. Ndipo ife tinkakhoza kufika mu gawo la nthaka lowoneka loyenera, Bambo Mc Anally ndi inemwini. Ndipo ife tinkakhoza kuwona malo omwe ankawoneka ngati, mu maenje aang'ono, mmene ngalande yaing'ono, zomwe iwo amazitcha "zokokoloka." Ndipo ine. . . Iye ankakhoza kunditengera ine kumeneko ndi kumakandipangitsa ine kuti ndiziperesa mchenga ndipo "psyfuu," kuwuwuzira iwo. Ndiye nkuwuperesa ndi "psyfuu," kuwuwuzira iwo. Ndipo ine ndinkadabwa chifukwa chomwe iye ankachitira izo. Ndinadzapeza kuti, inu mukuona, pamene iwe ukuwuzira mchengawo, iwo umapepuka. Ndipo zonse, ngakhale mpaka nkala, ndi wo pepuka kuposa golide. Golide ndi wolemera kuposa nkala. Kotero pamene iwe ukuwuzira, zitsulo zina zonse ndi mchenga ndi litsiro zimawuluzikapo, koma golide amatsalira pansipo. Chotero, ngati inu muli ndi zokokoloka zina zochokera mu mtunda kuno, izo zimasonyeza kuti pali kamlozo ka golide penapake pamwamba apo. Mvula iyi yakokolola zidutsa zazing'ono izo

nkuzichotsapo. Chotero ndiye ife timatenga zokumbira ndi zina zotero, ndi kulikumba phirilo chokwera, pafupifupi, kuyesera kuti timupeze golide uyu. Kuboola maenje mu nthaka, kuwakumba iwo. Kuikamo zophulitsira, ndi kuphulitsa pamenepo. Kupitiriza kuphulitsa dzenjelo, kupita pansi mpaka ife titapeza, kuti tipeze msempha waukulu. Tsopano, ndiko komwe ife timakutcha “kufufuza.”

<sup>18</sup> Ndipo usikuuno ife tikuyesera kuti tiwatenge Mawu a Mulungu, ndi kuwagwiritsa Iwo ntchito mwa mphamvu ya Mzimu Woyera, kuti tipemerere zosayanjanitsika zonse ndi zokaikira kutali ndi ife, zinthu zonse izo zazing’ono zopyapyala zopepuka zomwe ziribe maziko aliwonse, ziribe kulemera kulikonse mu moyo wathu, ife tikufuna kuti tiziwuluzire izo zonse kutali kuti ife tikawupeze Msempha waulemerero uwu. Msempha umenewo ndiwo Khristu.

<sup>19</sup> Ndipo tsopano Mulungu atatithandiza ife pamene ife tikuwerenga ndi kuphunzira mu Mawu Ake. Mitu itatu yotsiriza, ya mmbuyomu, pafupifupi, ife takhala tikuyankhula za kumva, pakali pano ndiyeno, Melkizedeki.

<sup>20</sup> Tsopano, ine ndikuganiza Paulo akupereka kutanthauzira kolondola.

*Pakuti Melkizedeki uyu, mfumu ya Salemu, . . .*

“Mfumu ya Salemu.” Ndipo sikolala wa Baibulo aliyense akudziwa kuti Salemu anali poyamba . . . Yerusalemu poyamba ankatchedwa “Salemu.” Ndipo Iye anali Mfumu ya Yerusalemu. Mpenyeni Iye.

*. . . wansembe wa Mulungu wammwambamwamba,  
(uyu ndiye wokhalira pakati), yemwe anakomana naye  
Abrahamu. . .*

Ine ndikufuna kuti nditenge m’badwo Wake, Munthu wamkulu uyu, kuti inu mudziwe yemwe Iye ali, poyamba, ndiyeno inu . . . ife tipitirira ndi nkhaniyo.

*. . . akubwerera kuchokera kokapha mafumu, ndipo  
anamudalitsa iye;*

*Kwa yemwe . . . Abrahamu anampatsa gawo  
lakhumi . . . poyamba . . . mwa kutanthauzira Mfumu  
ya chilungamo, . . .*

Tsopano penyani, “Chilungamo.” Tsopano, ife tiri nacho chilungamo chathu chathu, ife tiri nacho chilungamo chodzipangitsa, tiri nacho chilungamo chopotozedwa, mitundu yonse. Koma pali chilungamo chimodzi chenicheni, ndipo chilungamo chimenecho chimachokera kwa Mulungu. Ndipo Munthu uyu anali Mfumu ya chilungamo. Kodi Iye angakhoze kukhala ali ndani?

<sup>21</sup> Tsopano, Iye anali Mfumu ya chilungamo, Mfumu ya Yerusalemu, Mfumu ya chilungamo, Mfumu ya mtendere.

Yesu ankatchedwa, “Kalonga wa mtendere.” Ndipo kalonga ndi mwana wa mfumu. Chotero, Munthu uyu anali Mfumu ya mtendere, ndiye Iye ayenera kuti anali Atate wa Kalonga wa mtendere. Mukuzimvetsa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>22</sup> Tsopano tiyeni tiwone, titenge mbadwo Wake patsogolo pang’ono, kuti tiwone komwe ife tikupita.

*Wopanda atate, . . .*

Tsopano, Yesu anali nawo Atate. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Zedi.

*. . . iye anali wopanda amayi, . . .*

Yesu anali nawo amake. Koma Munthu uyu analibe bambo ngakhale amake.

*. . . wopanda fuko, . . .*

Iye analibe konse aliyense yemwe Iye anachokerako, fuko lirilonse. Iye nthawizonse analipo. “Wopanda fuko.”

*. . . wopanda ngakhale chiyambi cha masiku, . . .*

Iye analibe konse nthawi iliyonse yomwe Iye anayambirapo.

*. . . ngakhale mathero a moyo; . . .*

Uyo sakanakhoza kukhala china chakenso koma Mulungu. Ndizo zonse zomwe Izo zikanakhala ziri.

<sup>23</sup> Tsopano, tsopano ngati inu mungazindikire pamene ife tikuwerenga ndime yotsatira. Mukuona? “Poyamba, pokhala mwa kutanthauzira, Mfumu ya chilungamo.” Apo si pamene ine ndikufuna ndichitepo. N—ndime ya 3, “Ngakhale mathero a moyo.”

*. . . koma anapangidwa monga ngati Mwana wa Mulungu; . . .*

Tsopano, Iye sanali Mwana wa Mulungu, pakuti, ngati Iye akanakhala Mwana, Iye anali ndi chiyambi. Ndipo Munthu uyu anali wopanda chiyambi. Ngati Iye anali Mwana, iye ankayenera kuti akhale nawo onse abambo ndi amake. “Ndipo Munthu uyu analibe ngakhale abambo kapena amake. Koma Iye anapangidwa *mofanana ngati* Mwana wa Mulungu.”

*. . . akanali wansembe mopitirirabe.*

<sup>24</sup> Tsopano, Dr. Scofield akuyesera kunena, kuti, “Uwo unali unsembe, wotchedwa, ‘Unsembe wa Melkizedeki.’”

Koma ine ndikufuna kuti ndingokutengerani inu pa zimenezo kwa maminiti pang’ono okha. Ngati uwo unali unsembe, ndiye iwo unayenera kukhala nacho chiyambi, ndipo iwo unayenera kukhala nawo mathero. Koma, “Uyu analibe chiyambi kapena mathero aliwonse.” Ndipo iye sananene kuti iye anakomana ndi unsembe. Iye anakomana ndi Mwamuna, ndipo anamutcha dzina lake “Melkizedeki.” Iye anali Munthu,

osati chipembedzo, osati u—u—unsembe kapena utate. Iye anali mwamtheradi Munthu dzina lake Melkizedeki, yemwe anali Mfumu ya Yerusalemu. Osati unsembe, koma Mfumu wopanda bambo. Unsembe sumakhala ndi bambo. “Ndipo Munthu uyu anali wopanda bambo, wopanda amayi, wopanda chiyambi cha masiku kapena mathero a moyo.” Tsopano, Mwana wa Mulungu. . .

<sup>25</sup> Yemwe uyu anali, uyu anali Yehova. Uyu anali Mulungu Wamphamvuzonse Mwiniwake. Iye sakanakhoza kukhala wina.

<sup>26</sup> Tsopano zindikirani, “Iye alipobe kwanthawizonse.” Iye ali nawo umboni apa, kuti, “Iye alimoyo. Iye samafa konse.” Iye sanayambe wateropo. Iye sanayambe wakhala china chakenso koma wamoyo. “Iye alipobe kwanthawizonse.”

<sup>27</sup> Tsopano, Yesu anapangidwa, mofanizira kwa Iye. Tsopano, chifukwa chomwe apo panali kusiyana pakati pa Mulungu ndi Yesu: Yesu anali ndi chiyambi; Mulungu analibe chiyambi. Melkizedeki analibe chiyambi, ndipo Yesu anali ndi chiyambi. Koma Yesu anapangidwa, mofanizira kwa Iye. “Wansembe, alipobe kwanthawizonse.”

<sup>28</sup> Tsopano, pamene Melkizedeki anali pa dziko lapansi, iye sanali kanthu mu dziko koma—Yehova Mulungu atawonetseredwa mwa chilengedwe, Iye anali ali kuno monga fiofane. Abrahamu anakomana naye Iye kamodzi, mu hema wake. Ndipo monga ife tinanena mmawa uja, “Abrahamu anamuzindikira Iye. Ndipo Iye anamuza Abrahamu chomwe Iye anali kuti akachite, chifukwa Iye sakanati amusiye wolandira wa dziko wakhungu kwa zinthu zomwe Iye amati akazichite.”

<sup>29</sup> Mundirole ine ndiime apa kwa miniti, kuti ndinene, Mulungu akadali nalobe lingaliro lomwelo pa Mpingo Wake. Inu simuli ana a mdima. Ndinu ana a Kuwala. Ndipo. . . ife amene. . . “Odala ali ofatsa, pakuti iwo adzalandira dziko lapansi.” Ndipo akanatero Mulungu, Yemwe anachita k—kwa Abrahamu, yemwe anali woti alandire dziko lapansi. . . Ndipo Iye anati, “Ine sindimubisila zinthu izi munthu yemwe ati alandire dziko lapansi.” Ndi mochuluka bwanji Iye ati aululire zinsinsi Zake kwa Mpingo Wake womwe uti ulandire dziko lapansi!

<sup>30</sup> Daniele anati, “Mu tsiku limenelo iwo adzathamangira uku ndi uko, chidziwitso chidzachuluka.” Ndipo iye anati, “Anzeru adzamudziwa Mulungu wawo, mu tsiku limenelo, ndipo azidzachita zopambana zazikulu mu tsiku limenelo. Koma oipa sazidzamudziwa Mulungu wa Kumwamba.” Iwo akumudziwa Iye mu mawonekedwe ndi mwa mipingu, monga phunziro lathu loyamba linanena, koma iwo sakumudziwa Iye mwa njira ya ungwiro.

<sup>31</sup> Ndipo Mulungu angakhoze kokha kugwira ntchito kudzera mu ungwiro, chifukwa Iye ndi Wangwiro. Lodala likhale Dzina

Lake. Iwo uyenera kukhala uli mpita wangwiro umene Mulungu amagwiriramo ntchito, chifukwa Iye sangakhoze kuchita kanthu kenanso koma kugwira ntchito kudzera mu ungwiro. Iye sangakhoze kudziipitsa Iyeyekha mwa njira iliyonse. Ndiyeno ndicho chifukwa Yesu anabwera kuti adzachotse machimo athu, kuti ife tikakhoze kukhalitsidwa angwiro, kuti Mulungu azikhoza kumagwira ntchito kupyolera mu Mpingo Wake. Apo ndi pamene pagona chinsinsi.

Apo ndi pamene dziko liri lakhungu. Apo ndi pamene iwo akufuna kunena, kuti, “Iwe wasokonezeka malingaliro ako.” Apo ndi pamene iwo akufuna azinena kuti, “Iwe sukudziwa zomwe iwe ukuzinena.”

Chifukwa, “Zinthu za Ambuye ndi zopusa kwa nzeru ya dziko lino. Koma zinthu za mdziko ndi zachithupithupi kwa wokhulupirira.” Chotero, ndinu munthu wosiyana, inu mukukhala moyo mu dera losiyana. Inu simuli panonso a mdziko lino. Inu mwadutsa kuchokera ku moyo uno mwapita ku Moyo watsopano.

<sup>32</sup> Chotero, Mulungu amaululira, osati kwa dziko, osati kwa owerenga maganizo, osati kwa atumiki ophunzira, koma kwa odzichepetsa mu mtima. Anthu Ake omwe ali ofatsa, Iye aziwululira zinsinsi za zinthu zazikulu za Mulungu, kwa iwo. Inu mukuziona izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>33</sup> Tsopano, tsopano, Abrahamu anali woti alandire dziko. Kupyolera mu Mbewu ya Abrahamu mafuko onse anali woti adalitsidwe. Kotero Mulungu anabwera pansi ndipo anadzayankhula kwa iye, mwa mawonekedwe a Munthu.

Tsopano, Mulungu nthawizonse wakhala ali pa dziko lapansi. Mulungu sanayambe walisiyapo dziko lapansi. Ngati Iye akanati alisiye konse dziko lapansi, ine sindikudziwa chomwe chikanachitika kwa ilo. Koma Mulungu nthawizonse wakhala ali kuno mwa mawonekedwe ena ake. O, lemekezani Dzina Lake!

<sup>34</sup> Iye anali ndi ana mu chipululu, akubwera kuchokera ku Igupto, mwa mawonekedwe a Kuwala. Iye anayankhula kwa Abrahamu mwa mawonekedwe a Munthu. Iye anayankhula kwa Mose mwa mawonekedwe a Munthu. Iye anayankhula kwa Mpingo mwa mawonekedwe a Munthu, Mwana Wake, Khristu Yesu.

Ndipo Iye akuyankhula kupyolera mu Mpingo Wake lero, kupyolera mu Mpingo wodzozedwa wa Mulungu wamoyo, kupyolera mu zotengera za dongo. “Inu ndinu nthambi. Ine ndine Mpesa.” Mulungu akuyankhulabe, ndipo dziko likumamuwona Yesu pamene inu mukumuwonetsera Iye. Umo ndi momwe dziko lirili. . . “Ndinu akalata olembedwa, owerengedwa ndi anthu onse.” Moyo wanu umafotokoza chomwe inu muli.



35 Tsopano, Abrahamu uyu ali pa ulendo wake, akubwerera. Ife tibwerera mmbuyo ndi kukawerenga za Iye, mphindi pang'ono chabe, mu Bukhu la Genesis. Mu mutu wa 14 wa Genesis, ine ndikukhulupirira ipo pali. O, kukongola kwake nkhanayi ili! Tsopano, ife tonse tikudziwa za Abrahamu, momwe Mulungu anamuitanira iye kuchokera ku dziko la Akaldia ndi mzinda wa Uru, ndipo anamuza iye kuti adzipatule yekha kwa oyanjana naye ake.

Mulungu amaitana amuna kapena akazi, Iye amawaitanira ku kudzipatula.

36 Tsopano, ndilo lomwe liri vuto ndi mipingo lero, iyo siikufuna kuti idzipatule yokha kwa akale achithupithupi okhu-...osakhulupirira. Ndicho chifukwa ife sitingakhoze kupita patali paliponse. Ife timangolowa mu kuyendela kwa chithupithupi kumodzi, ndipo i—ife timati, “O, Jim ndi munthu wabwino, ngati iye amwa. Ngati iye. . . Ndipo ine ndimapita ndi iye ku chipinda cha pulu, koma ine sindimasewera pulu. I—i—ine ndimapita naye iye ku phwando. Iwo amanena nthabwala zauve, ndi zina zotero, koma ine sindinena iliyonse.”

37 “Tulukani pakati pawo.” Ndiko kulondola. “Dzipatuleni nokha. Musati muzikhudza zinthu zawo zosayera, ndipo ine ndikulandirani inu,” atero Ambuye. “Musati muzimangidwa goli limodzi ndi osakhulupirira, osafanana kukhala pagoli limodzi nawo.” Musati muzichita zimenezo. Muzidzipatula nokha.

38 Ndipo Mulungu anamuitana Abrahamu kuti adzipatule yekha kuchokera kwa apachibale ake onse, ndi kuti aziyenda ndi Iye. M'bale, nthawizina izo zimatanthauza kuwusiya mpingo. Izo zinatanthauza chomwecho kwa Paulo. Iye anayenera kuti awusiye mpingo wake. Izo zimatanthauza chomwecho kwa ambiri. Nthawizina izo zimatanthauza kuchoka kwanu. Nthawizina izo zimatanthauza kuwasiya abambo ndi amayi, ndi kusawasamala onse. Ine sindikutanthauza kunena kuti zimatero nthawizonse, koma nthawizina izo zimatero. Izo zimatanthauza kuti iwe uyenera kutenga chirichonse pakati pa iwe ndi Mulungu, ndi kumayenda ndi Iye wekha. O, chiyanjano chodala, chokoma icho, chiyanjano icho chomwe inu mumakhala nacho pamene inu mulekanitsidwa ndi chinthu chanu, inueni, kwa zinthu za mdziko ndi okhulupirira mwachithupithupi omwe amakutonzani inu, ndi kumayenda nokha ndi Khristu!

39 Ndi nthawi zingati zomwe ine ndamuthokoza Mulungu! Iye anati, “Ine ndikupatsani inu abambo ndi amayi mu dziko liripo ili. Ine ndikupatsani inu abwenzi ndi oyanjana nawo. Ndipo ine sindidzakusiyani konse inu, ngakhalenso ine kusakusamalani inu. Ngakhale dziko lonse litatembenezira nsana wake kwa inu, ine ndidzapita nanu, mpaka kumathero a njira.”

40 Ndi mwayi wodala bwanji, kuti munthu ali nacho chitsutso icho choti azimutsatira Ambuye Yesu, kuti adzipatule

yekha kuchoka kwa oyanjana nawo mwachithupithupi, kuti aziwatsatira Ambuye. Ndipo ngati munthu aliyense awoneka kuti alibe khalidwe moyenera, ndi kumadziwonetsera okha ngati Akhristu, koma nkumakonda zinthu zachithupithupi, ndi kwabwino kuti inu mufune mzanu wina nthawi yomweyo. Uko nkulondola. Ndipo ngati palibe wina ati aziyenda ndi inu, alipo Wina yemwe analonjeza kuti aziyenda ndi inu. Ndiye, Ambuye Yesu wodala, Iye aziyenda ndi inu.

<sup>41</sup> Mulungu anamuuza Abrahamu kuti, “Adzipatule yekha.” Ndipo basi monga waumunthu yemwe Abrahamu anali, iye anawatenga abambo ake limodzi naye, iye anamatenga mwana wa m’bale wake, mdzukulu wake; onse atakangamira pa iye. Ndipo Mulungu sanamudalitse konse iye mpaka pamene iye anachita zomwe Mulungu anamuuza iye kuti achite.

<sup>42</sup> Ine sindikunena kuti inu sindinu Mkhristu. Apo, ine sindikumupanga winawake kusakhala mkhristu. Koma ine ndinene ichi, kuti ngati Mulungu anakuuzani inu chinachake choti muchichite, Iye sadzakudalitsani konse inu mpaka inu mutachichita icho. Ine ndiri pa guwa usikuuno ndi chimodzi cha zinthu zimenezo zikugwira pa ine. Misonkhano yanga siinakhale chomwe iyo imayenera kuti izikhala, kwa zaka ziwiri zapitazi. Ndi chifukwa kuti ine ndawalephera Ambuye. Iye anandiuza ine kuti, “Pita ku Afrika, ndipo kenako ku India.” Ndi izi apa, ndinazilemba apa pomwe, mu chikutiro cha Bukhu ili, pomwe pano.

<sup>43</sup> Amenenjala anandiimbira ine, anati, “Asiyeni Maafricana awo apite. India wakonzeka.”

<sup>44</sup> Mzimu Woyera unakomana nane, unati, “Iwe upita ku Afrika momwe ine ndinakuuza iwe kuti utero.”

<sup>45</sup> Ndipo chaka china chinadutsa. Ndipo mamananjala. . . Ine ndinaiwala za Izo. Iye anati, “Ife tikupita ku India. Matikiti ali kale pano.”

<sup>46</sup> Ine ndinauyambapo, ndinaiwala Izo mpaka ine nditafika ku Lisbon. Usiku wina, apo, ine ndinkaganiza kuti ine ndinali kufa. Mmawa wotsatira ine ndinayamba, kupita ku chipinda chosambira, kuti ndikasambe. O, ine ndinali wodwala kwambiri, ine ndinkalephera ngakhale kuti ndiime. Apo, Kuwala kuja kutapachikika apo mu chipinda chosambira, anati, “Ine ndimaganiza ndinakuuza iwe kuti, ‘Upite ku Afrika, poyamba.’”

<sup>47</sup> Misonkhano yanga yakhala ikulephereka pang’onopang’ono kuchokera nthawi imeneyo. Ngakhale ine ndinapita ku India, ndi pafupi theka la milioni ataima pamenepo, koma uko sikunali kuchita zomwe Mulungu anati ndichite. Ine ndikumverera kuti misonkhano yanga siidzakhala yopambana mpaka ine nditabwerera molunjika kumene ndi kukachikonza chinthu chimenecho. Ziribe kanthu zomwe ine ndingachite, ndi Afrika,

poyamba, chifukwa iwe uyenera kuzichita izo. Apo pali Mawu a Mulungu Amuyaya, ali pamenepo. Ine ndinkadziwa bwino kuposa izo. Koma ine ndiyenera kuti ndibwererekonso. Ndipo ine ndikumverera kuti chaka chikubwera ichi ndi nthawi yomwe ine nditi ndituluke mu chigobacho, mwa kuthandiza kwa Ambuye.

<sup>48</sup> Uthenga waulemerero, wachikale uwu womwe wakhala ukukula mophweka, monga mtengo wa mgwalangwa, koma ine ndikukhulupirira kuti iwo watsala pang'ono kuti ukonzekere kuyangitsa nthambi zake tsopano. Ine ndikukhulupirira Izo, Uthenga waukulu uwu ndi chinthu chachikuluchi. Ine ndikukhulupirira kuti Ambuye atilola ife kuti tiligwedeze dziko kachiwiri kwa ulemerero wa Mulungu.

<sup>49</sup> Iwe umayenera kuchita zomwe Mulungu wakuuza kuti iwe uzichite. Ndipo Abrahamu anapitirira nazobe, anawatenga abale ake limodzi naye. Iye ankawakonda iwo. Ndilo gawo la umunthu. Koma patapita kanthawi, pang'ono ndi pang'ono, bambo ake anafa ndipo iye anawaika iwo. Ndiye iye anatsala ndi mdzukulu wake, kenako makangano ndi kutsutsana zinabwerapo. Ndipo, potsiriza, Loti anatenga kusankha kwake ndipo anapita uko nakalowa mu Sodomu. Ndipo inu mukuzindikira Abrahamu, iye sanakangane naye Loti. Iye anati, "Ife ndi abale. Ife tisati tizikangana. Koma iwe kweza mutu wako ndipo iwe upite kulikonse komwe iwe ukufuna kuti upiteko. Ngati iwe upita kummawa, ine ndipita kumadzulo. Iwe ukapita kumpoto, ine ndipita kummwera." Ndilo khalidwe Lachikhristu, kukhala wololera kumuponse munthu winayo chopambana cha mgwirizano. Nthawizonse kuchipereka icho kwa iye, kumulola iye kuti atenge kusankha kwake.

<sup>50</sup> Chifukwa chiani? Nchiani chinamupangitsa Abrahamu kuchita izo? Iye ankadziwa kuti iye analonjezedwa ndi Mulungu kuti iye akanati adzalandire chinthu chonsecho, mulimonse. Amen. Koteru, ndiye, hema kapena khumbi, ife tizisamala chifukwa chiani? Chinthu chonsecho ndi chathu. "Odala ali ofatsa pakuti iwo adzalandira dziko lapansi." Ilo lonse ndi lathu. Mulungu ananena chomwecho. Chotero zimpatsani munthu kusankha kopambana, ngati iye akufuna kutero. Mwinamwake izo ndi zonse zomwe iye ati adzapeze konse. Koma izo zonse ndi zanu, olandira a chipulumutso mwa lonjezo. Izo zonse ndi zanu.

<sup>51</sup> Chotero, Sara, mkazi wokongola kwambiri mu dzikolo, iye anakhala kumeneko ku mbali ya phiri ndi mwamuna wake monga momwe iye ankayenera kumachitira. Iye mwawamba, chabwino, mwinamwake ankavala diresi yawamba ya kaliko, kapena chirichonse chomwe inu mukanafuna kuitcha iyo. Pamene, Akazi a Loti ankavala ngati wamamilioni. Ndipo mwamuna wake anali meya wa mzindawo. Iye anali woweruza yemwe ankakhala ku chipata. Iye anali nacho chirichonse; ankakhala nawo ku mabwalo onse azosoka ndi maphwando a

njuga omwe analipo mu Sodomu ndi Gomora. Koma Sara anali kukondweretsedwa mochulukwa kumakhala ndi mwamuna wake mwa kupeza koperewera, ndi kumadziwa kuti iye anali mu chifuniro cha Mulungu, kuposa kusangalala ndi chuma cha... kapena zosangalatsa za chuma chakanthawi. Ndiko kulondola. Ndi pamene Mulungu amadzachezera.

<sup>52</sup> Ndipo tsiku lina, inu, motsimikiza basi monga pamene inu mutenga msewu wolakwika, izo zidzakupezani inu tsiku lina. Inu mukhoza kuganiza kuti mukupitirira nazo bwino bwino. Inu mukhoza kumaganiza kuti mukudutsa nazo, koma inu simuli. Izo zikhoza kumawoneka ngati izo zonse zaphimbidwa ponse, koma izo siziri zophimbidwa ponse. Mulungu akudziwa chirichonse. Iye akudziwa ngati inu mukutanthauza kwenikweni mu kuvomereza kwanuko kapena ayi. Iye akudziwa ngati inu mukutanthauza kwenikweni kuti inu mukumukhulupirira Iye ndipo mwapululumutsidwa, ndipo mwamulandira Iye, ndipo inu muli okufa kwa zinthu za mdziko, ndipo inu muli amoyo mwa Khristu. Iye akuzidziwa zimenezo.

<sup>53</sup> Tsopano, ife tikuzindikira Abrahamu, ine ndikufuna kuti inu muzindikire mzimu weniweni uwo. O, chinthu chodala chonsecho apa ndi chisomo. Ine ndikufuna kuti inu muwerenge ndi ine tsopano kuyambira pa mutu wa 14 wa...Eksodo, mphindi yokha.

<sup>54</sup> Tsopano, chinthu choyamba chomwe chinachitika pamene iwo anakafika uko, Loti analowa mu vuto. Bwanji? Iye anali kunjwa kwa chifuniro cha Mulungu. Ndipo ngati iwe ulowa mu vuto pamene iwe uli mu chifuniro cha Mulungu, Mulungu amakuthandiza iwe kuti uchokemo. Koma ngati iwe uli mu vuto, kunjwa kwa chifuniro cha Mulungu, pali chinthu chimodzi chokha choti uchite, bwerera mu chifuniro cha Mulungu kachiwiri.

<sup>55</sup> Tsopano, mafumu onse anadzisonkhanitsa palimodzi, ndipo iwo analingalira kuti zigwa izo uko zinali zamadzi mwabwino, ndipo iwo akanangopita uko ndi kukamutenga Sodomu wakale wamng'ono uyu, Gomora, kumulanda iye. Ndipo iwo anatero. Ndipo pamene iwo anapita uko ndi kukamulanda iye, iwo anamutenga Loti limodzi nawo.

<sup>56</sup> Tsopano ine ndikufuna kuti inu muuzindikire Mzimu wa Khristu apa mwa Abrahamu. Tsopano zindikirani ndime ya 14.

*Ndipo pamene Abrahamu anamva kuti m'bale wake... (Mukumvetsa izi?)... m'bale wake anali atatengedwera mogwidwa, iye anawapatsa zida antchito ake ophunzitsidwa, obadwira mu nyumba yake yomwe, firii handiredi ndi eyitini, ndipo anawatsatira iwo mpaka ku Dani.*

<sup>57</sup> O, ganizo lodala lake la chisomo! Abrahamu, pamene m'bale wake, ngakhale atagwa ku chisomo, ngakhale anali mu chikhalidwe chakugwa ichi; pamene iye anamva kuti dziko linali

litamugwira iye apo, ndipo anamugwira iye ndipo amutengera iye kutali, kuti akamuphe iye, Abrahamu anachita mwa Mzimu wa Khristu. Iye anabwera ndipo anawapatsa zida amuna ake onse omwe anabadwira mu nyumba yake, ndipo anauyamba mowatsatira iwo, ndipo anawathamangira iwo njira yonse mpaka ku Dani. Ndipo Dani ndilo gawo lakutali kwambiri la Palestina, “Dani mpaka ku Beresheba,” kuchokera ku mapeto amodzi mpaka ku ena. Ndipo icho ndi choimira cha Khristu, pamene Iye anawona kuti dziko linali litatenga . . . linali litagwa, kuti Iye anamuthamangitsa mdani mpaka ku mapeto, kuti akaulandire ubwerere mtundu wakugwa wa Adamu.

<sup>58</sup> Ine ndikufuna kuti inu muzindikire ndime yotsatirayi, kukoma kwake apa Mzimu ukuyankhula kudzera mwa iye. Chabwino, ndime ya 15 tsopano.

*Ndipo iye anabwerera nawo onse (onse) akatundu, ndiponso anamubweretsa aponso m'bale wake Loti, ndi akatundu ake, ndi akazi nawonso, ndi anthu.*

<sup>59</sup> Pamene Abrahamu anayamba kumutsatira mdani yemwe anali atamutenga m'bale wake, iye anamuthamangitsa iye njira yonse kudutsa mu fukolo, mpaka ku Dani, ndipo anabwerera nacho chirichonse chomwe iye anachitaya mu kugwako.

<sup>60</sup> Chithunzi chake chokongola cha Khristu, yemwe anamva kuchokera Kumwamba kuti ife tinali titataika ndipo anabwera ndipo anamuthamangitsa mdaniyo, njira yonse mpaka ku gehena, ndipo anakaitenga miyoyo yotaika ndipo anatibweretsako ife ndi kutibwezeretsa ife kwa chirichonse chomwe ife tinali nacho kusanachitike kugwako! Ife, obwererambuyo, ife amene tinabadwa kuti tidzakhale ana aamuna a Mulungu, omwe tinapotozedwa nkukhala ana a Mdierekezi, ndipo tinapanga, tinatsatira zinthu za mdziko, ndipo tinachita zolakwika, ndi kumakhala modzikonda monga Loti anachitira, kugulitsa mafulu athu obadwa nawo ndi kupita motsatira zinthu za mdziko. Khristu anabwera pansipa. Ngakhale tinagwa; Mulungu, podziwa pachiyambi yemwe akanati adzapulumutsidwe ndi yemwe sakanati, chotero anabwera pansu ndipo anamuthamangitsa mdaniyo kudzera mu moyo, kudzera mu imfa, kudzera mu paradiso, mpaka ku gehena. Ndipo njira yonse kuchokera ku Ulemerero mpaka ku gehena, ndipo anakalandako—mphamvu za gehena, ndi mafungulo kuwachotsa kwa Mdierekezi, ndipo anauka kachiwiri, ndipo anawubwezeretsanso mtundu wa anthu, kuti iye akhoze kukhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu kachiwiri.

<sup>61</sup> Mukuwuona Mzimu mwa Abrahamu apo, Mzimu wa Khristu ukubwera ndi iye?

<sup>62</sup> Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire mopitirira pang'ono, pamene ife tikuwerenga.

*Ndipo mfumu ya Sodomu inapita uko kukakomana naye iye atabwerera kale kokapha mfumu iyi Chedorlaomere, ndi...mafumu... anali ndi iye, mu chigwa cha Shave, kumene kuli ku chigwa cha mfumu.*

<sup>63</sup> Iwo anapita uko. Mfumu ya Sodomu inabweretsedwakonso. M'bale wake anabweretsedwakonso. Ana anabweretsedwakonso. Ndipo apa anapita uko mafumu kuti akakomane naye iye. Ndipo, aponso, apa ndi pamene ine ndikufuna kuti ndifikepo, uthengawu tsopano. Penyani apa.

*Ndi—ndipo Melkizedeki, mfumu ya Salemu (Mfumu ya Yerusalemu, Mfumu ya mtendere) anabweretsa apo mkate ndi vinyo: ndipo iye anali wansembe wa Mulungu wammwambamwamba.*

*Ndipo iye anamudalitsa iye, ndipo anati, Wodalitsidwa akhale Abrahamu wa Mulungu wammwambamwamba, mwiniwake wa miyamba ndi dziko lapansi:*

<sup>64</sup> Melkizedeki, Mfumu ya Salemu, nayenso anadziimira Iyeyekha pakati pa mafumu ena. Ndipo zindikirani, nkhoodoyo inali itatha, Mzimu wa Mulungu mwa Abrahamu, wa Khristu, womwe unamubweretsanso m'bale wake wakugwa, ndiye nkumubwezeretsanso iye ku chikhalidwe chake chamoyenera, kwa zonse zomwe iye anali atazitaya. Iye anazibwezeretsanso izo. Ndipo pamene iye anatero, Iye anabweretsa uko mkate ndi vinyo, chiyanjano. Kodi inu simukutha kuwona yemwe Melkizedeki uyo anali? Iye anali Mulungu. Anabweretsa uko mgonero, nkhoodo itatha.

<sup>65</sup> Tsopano tiyeni ife titembenuzire kachiwiri, ku Mateyu 26:26, mofulumira ndithu, ndi kuwona zomwe Yesu ananena apa pa izo. Mu Bukhu la Mateyu, mutu wa 26 ndiponso ndime ya 26, ife tikufuna kuti tiwerenge pang'ono pokha apa. Chabwino, Mateyu 26:26.

*Ndiye anadza Yesu limodzi ndi iwo ku malo otchedwa Gologota, Gologota...kapena Getsemane, ine ndikutanthauza, ndipo ananena kwa ophunzira ake, Khalani inu pano, pamene ine ndikupita uko kuti ndikapemphere.*

<sup>66</sup> Ine ndikukhulupirira ine ndatenga Lemba lolakwika. Mateyu, twente-... ndime ya 26 ya mutu wa 26. Ngati winawake ali napo, andiwerengere ine apo, ngati i—ngati inu mungapapeze apo. Miniti yokha. Ichi ndi choimira chokongola apa. Ine sindikufuna kuti inu muchiphonye icho. Apa ife tiri. Izo zapapeza apo, mlongo.

*Ndipo pamene iwo anali kudya, Yesu anatenga mkate, ndipo anaudalitsa iwo, . . .*

Kodi icho chinali chiani? Nkhondo inali itatha.

*...ananyema iwo, ndipo anaupereka iwo kwa ophunzira ake, ndipo anati, Tengani, ndipo idyani; ili ndi thupi langa.*

<sup>67</sup> Mukumuona Melkizedeki uyo? Mazana a zaka mmbuyo, pamene Iye anakomana ndi Abrahamu, nkhondo itatha, Iye anapereka mkate ndi vinyo. Ndipo apa Yesu akuwapatsa ophunzira, nkhondo Yake yolimba itatha, Iye anawapatsa iwo mkate ndi vinyo. Penyani. Penyani Kudza kwamtsogolo.

*Ndipo iye anatenga chikho, n—ndipo anapereka mayamiko, ndipo anachipereka icho kwa iwo, nanena, Imwani inu iye yense.*

*Pakuti uwu ndi mwazi wanga wa pangano latsopano, umene wakhetsedwera kwa...machimo ndi kuchotsa kwa machimo.*

*Koma ine ndikuti kwa inu, ine sindidzamwanso kuchokera pano wa chipatso cha mpesa, kufikira tsiku ilo pamene ine ndidzamumwa iye katsopano, limodzi ndi inu mu ufumu wa Atate wanga.*

<sup>68</sup> Ife tiri mu nkhondo tsopano. Ife tikutsatira m'bale wathu wokugwa, yemwe Mulungu, asanaikidwe maziko a dziko, anamuwona ndipo anamukonzeratu ku Moyo Wamuyaya. Ndipo zinthu za mdziko zakhala zitamugwira iye mu kamvulumvulu. Iye ali uko mu mabungwe ndi makalasi, iye ndi mkazi wake, akuyenda chokwera ndi chotsika mmisewu, akusuta ndi kumwa ndi kusisitana, kuyesera kuti apezere mtendere. Ndipo Mzimu wa Khristu mwa ife, monga iwo ukanakhalira mwa Abrahamu, ife tapita momutsatira iye. Ndi zida zonse za Mulungu, Angelo a Mulungu amanga misasa motizungulira, ife tapita kuti tikamubweretse m'bale wathu wokugwa.

<sup>69</sup> Ndipo pamene nkhondo potsiriza ikhala itatha, ife tidzakakomana naye Melkizedeki kachiwiri, Mulungu adalitsidwe, yemwe anamudalitsa Abrahamu uko, ndipo anamupatsa iye mdalitso, ndipo anampatsa iye mkate ndi vinyo, mgonero. Ndipo pamene nkhondo ikhala itatha, ife tidzakakomana naye Iye. Iye omwe tiri olandira lonjezo la Abrahamu, olandira molumikizana ndi Khristu mu Ufumu, tidzakakomana naye Iye pa mapeto a msewu, ndi kudya mkate ndi vinyo, kachiwiri, pamene nkhondo yatha.

<sup>70</sup> Ndi ndani Melkizedeki uyu? “Iye yemwe anali wopanda atate, anali wopanda amayi, anali wopanda chiyambi cha masiku kapena mathero a moyo.” Iye adzakhala ali Kumeneko kuti adzapereke mgonero kachiwiri. Inu mukumvetsa izi? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>71</sup> Pamene ife timabwerapo, mausiku ena, pamene ife timabwera palimodzi ndi kutenga mgonero kuchokera mmanja a atumiki, kuimira kuti ife tikukhulupirira mu imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro cha Ambuye Yesu, kuti—chophimba

chija, thupi Lake lomwe Iye anali ataphimbidwamo, Mulungu. Iye timatenga izo, ngati choimira, “Ife tafa kwa zinthu za mdziko, ndipo ife takhala titabadwa katsopano mwa Mzimu.” Ndipo ife tikuyenda ndi Thupi la Khristu, okhulupirira onse palimodzi.

<sup>72</sup> Pamene nkondo yaikulu ikhala itatha, ndipo ife nkubwera aponso ndi Khristu, ife tidzatenga mgonero ndi Iye mu Ufumu wa Mulungu, katsopano; ndi kudya mnofu, ndi kumwa magazi a mposa kachiwiri, mu Ufumu wa Mulungu. O! Ndi ameneyo Melkizedeki. Ndi yemwe Iye anali.

<sup>73</sup> Tsopano tiyeni tiwerenge mopitirira pang’ono pokha apa za Iye, ndipo ndime ya 18.

*Ndipo Melkizedeki mfumu ya Salemu anabweretsa apo mkate ndi vinyo: . . . (Inu mukumvetsa izo?) . . . ndipo iye anali wansembe wa Mulungu wammwambamwamba.*

*Ndipo iye anamudalitsa iye, ndipo anati, Wodalitsidwa akhale Abrahamu ndi Mulungu wammwambamwamba, mwini wa miyamba ndi dziko lapansi:*

*Ndipo iye anamudalitsa iye, . . . Ndipo iye anamudalitsa . . .*

*Ndipo wodalitsidwa akhale Mulungu wammwambamwamba, yemwe wawapereka adani ako mdzanja lako. Ndipo anamupatsa iye chachikhumi cha zonse.*

Iye analipira zachikhumi kwa Melkizedeki. Abrahamu anamupatsa Iye chachikhumi cha zofunkha zake.

<sup>74</sup> Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire apa pamene Paulo akupitirira, kupereka maziko kwa phunziro likubweralo tsopano.

*Ndipo mfumu ya Sodomu inati kwa Abrahamu, Ndipatse ine anthuwo, ndipo iwe dzitengere katunduyu kwa iwemwini.*

Tsopano, mfumu ya Sodomu inati, “Tsopano, iwe ungondebwezera ine ondimvera anga, ndipo iwe udzitetengere katunduyu kwa iwemwini.”

*Ndipo Abrahamu anati kwa mfumu ya Sodomu, ine ndakwezera mmwamba dzanja langa kwa AMBUYE, Mulungu wammwambamwamba, . . .*

*El Elyon, “mwini wa miyamba ndi dziko lapansi,” apo.*

*. . . Mulungu wammwambamwamba, mwini wa miyamba ndi dziko lapansi,*

*Kuti ine sinditenga kuchokera mphonje ngakhale mpaka chingwe cha nsapato, . . .*



Iye sikuti anali ndi kukopa kwakukulu kuti atengepo ndalama. Iye a nali kungofuna m'bale wake wokugwayo.

*... ndipo ine sinditenga kalikonse ka inu, kuwopa kuti inu mungati, ine ndamupangitsa Abrahamu kulemera:*

*Kupatula zokha zimene anyamata adya, ndi gawo la amuna omwe anapita ndi ine, . . .*

<sup>75</sup> Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muzindikire, Abrahamu anati, “Ine sinditenga kuyambira mphonje mpaka chingwe cha nsapato.” Iye sanamenyere nkondoyo, kuti apange ndalama zambiri. Ndipo nkondo zooni zenizeni sizimapangidwa ndi malingaliro odzifunira. Nkhondo sizimamenyedwa chifukwa cha ndalama. Nkhondo zimamenyedwa—pa zochititsa, pa mfundo. Amuna amamenya nkondo chifukwa cha mfundo. Ndipo pamene Abrahamu anapita uko kuti akamutenge Loti, iye sanapite uko chifukwa iye ankadziwa kuti iye akanakhoza kuwakwapula mafumuwo ndikukatenga katundu wawo yense, iye anapita chifukwa cha mfundo ya “kukapulumsa m'bale wake.”

<sup>76</sup> Ndipo mtumiki aliyense yemwe atumizidwa kwina pansu pa kudzoza kwa Mfumu ya Kumwamba, sangati apite pofuna ndalama; ngakhalenso sangati apite kuti akapange mipingo yaikulu, ngakhalenso sangapite kuti akapangitse zipembedzo. Iye angapite kokha pa mfundo imodzi, ndipo iyo ndiyo, “Kuti akamubweze m'bale wake wokugwa.” Kaya iye sapeza khobidi mu zopereka kapena iye satero, izo siziti zipange kusiyana kwakung'ono kwa iye.

<sup>77</sup> Monga ine ndikuti, “Nkhondo zenizeni zimamenyedwera ndi kukonzedwera pa mfundo ndipo osati chifukwa cha ndalama.” Ndipo amuna ndi akazi omwe amajowina mpingo ndi kubwera mu mpingo, kuti akhale otchuka, chifukwa a *Yonasi* ndi a kumeneko, kapena kusintha mpingo wawo kuchokera ku mpingo wawung'ono kupita ku mpingo wawukulu, inu mukuchita izo pa malingaliro odzikonda ndipo mfundo yolondola sili kuseri kwa izo. Inu muzikhala lolera kukaima kutsogolo kwa nkondo.

<sup>78</sup> Mu kachisi uyu pano, pamene zinthu zilakwika, ndipo inu amuna ndi inu akazi mukumathawa ndi kupita kwinakwake, kapena kumajomba mpaka mkangano wawung'onowo kapena kukwiwirana kutatha, pali chinachake cholakwika ndi chokuchitikirani chanu. Kulondola.

<sup>79</sup> Iye tiri ndi chizolowezi pano. Iye tiri—ife tiri ndi dongosolo pano. Mpingo uyu unakhazikitsidwa pa mfundo za Baibulo. Ngati pali winawake pano yemwe sakuchita bwino, ndipo inu mukuganiza kuti iwo sali, inu mupite kwa iye ndi kukayankhula naye iye. Ngati inu simungamuyanjanitse iye, ndiye tengani m'bale wina limodzi nanu, mmodzi kapena awiri ena. Ngati

iyе sati аyanjanitsidwe apo, ndiye zineneni izo kwa mpingo. Ndipo mpingo umuchotsa iye, kukhala opanda chiyanjano ndi iye. Ndipo Yesu anati, “Chirichonse chomwe inu muchimasula pa dziko lapansi, Ine ndichimasula Kumwamba.”

<sup>80</sup> Nchifukwa chake inu mumakhala ndi mavuto ochuluka kwambiri, chifukwa inu simumatsatira mfundo za Baibulo. Ngati winawake mu mpingo akuyambitsa chisokonezo, kapena chinachake chikuchitika molakwika, iyo si ntchito yanu kuti muzipita kumakayankhula za mwamuna ameneyo kapena mkazi ameneyo. Ndi ntchito yanu kuti mupite kwa mwamuna ameneyo kapena mkazi, ndi kukamuuzа iye kulakwitsа kwake. Limodzi ngati iye sati akumvereni inu, tengani winawakenso limodzi nanu. Iye akapanda kumvera zimenezo, ndiye mpingo umamumasula iye. Yesu anati, “Chimene inu muchimasula pa dziko lapansi, ine ndichimasula Kumwamba. Chimene inu muchimanga pa dziko lapansi, ine ndichimanga Kumwamba.” Izo ndi mphamvu za mpingo.

<sup>81</sup> Kuno si kale litali, mlaliki wabwino mzanga wa ine, iye anali ndi mnyamata, ndipo mnyamata ameneyo amakhala akupita ku mpingowo, mpingo wake womwe. Iye anafika pa malo omwe iye anayamba kumathamanga thamanga ndi msungwana wamng’ono yemwe ankasuta ndi kumamwa ndi kupitiriza nazo. Mlaliki anati, “Ndithudi, iyo ndi ntchito yake.” Mzanga kwambiri wapachifuwa kwa ine, ndi mnyamata wabwino. Koma iye anangotengeka yense ndi msungwana wina wamng’ono; ndipo iye anali atakwatiwapo, anali ndi ana ena, mwamuna wake alimoyo. Iye ankawopa kuti iwo akanati akhale ndi. . . mnyamata uyo akamakwatira iye. Chotero, m’baleyo anali atakhumudwa kwathunthu. Ndipo iye anati kwa ine, “M’bale Branham, ine ndikufuna kuti inu mupite kwa mnyamata *wakuti-n-wakuti* wanga. Ine ndikufuna kuti inu mukayankhule naye iye.”

<sup>82</sup> Ine ndinati, “M’bale. . .” Ine ndinatsala pang’ono kutchula dzina lake. “Inu muli nayo njira yabwinoko. Musati munditume ine. Ngati mnyamatayo sakukhala moyo wabwino, ndipo mpingo wamuwona iye akuchita zolakwika, ndiye ndi chinthu choti mpingowo uchite ntchito imeneyo. Izo zatsalira kwa mpingo. Ndipo mpingo upita uko ndi kukamuuzа iye.”

<sup>83</sup> Chotero iye anatenga m’bale, ndipo anapita ndipo anakamuuzа iye. Ndipo iye anabweza moto pa m’baleyo, kumudziwitsа iye kuti azimasamalira ku ntchito yake yake, kuti iyenso azikachita zomwezo. Iye anatenga m’bale wina, awiri ena, madikoni awiri anapita uko ndipo anamuuzа mnyamatayo. Iye sanati amvetsere kwa izo. Iwo anakazinena izo kwa mpingo. Ndipo iye sanabwere kwa mausiku angapo, kuti akayanjanitsidwire kwa mpingo tchimo lake litanenedwa kale kwa mpingo. Ndiye, mpingo unamumasula iye.

<sup>84</sup> Ndipo pafupi mwezi kuchokera apo iye anakanthidwira pansi ndi chibayo, ndipo adokotala anati, “Palibe mwayi mu dziko kuti iye akhale moyo.” Ndiye iye anakwawa nabwerera. Mulungu amadziwa momwe angachitire izo.

<sup>85</sup> Ife timayesera kuti tizichite izo mwa ifeeni, “O, inu muyenera kuti mumuchotse *wakuti-n-wakuti* mu mpingo. Inu mukuyenera kuti muchite *izi, izo, kapena zina*.” Kodi inu mwachita gawo lanu ngati mpingo pa izo? Ndi inu apo. Ndi njira yake yowapangitsira iwo kuti akwawe nabwerera, atembenezireni iwo kwa Mdierekezi nthawi ina.

<sup>86</sup> Kodi Paulo ananena chiani za munthu uyu uko yemwe ankagona ndi amayi ake omupeza? Iwo analephera kuti amuyanjanitse iye. Anati, “Mtembenuzireni iye kwa Mdierekezi.” Penyani zomwe zinachitika. Ndipo mu kalata yotsatira yomwe Paulo analemba, munthu uyu anali atawongoledwa. Zedi. Mulungu ali nayo njira yochitira zinthu izi, ngati ife titati tingotsatira malangizo Ake.

<sup>87</sup> Ngati chinachake chilakwika mu mpingo, ngati izo ziri pakati pa osonkhana, mmodzi aliyense wa inu abale. Ngati izo ziri pa gulu la madikoni, mmodzi wa inu madikoni asakukhala moyo wabwino, madikoni enawo abwere ndi kudzakhala ndi msonkhano, kuyesera kuti amuyanjanitse m'baleyo, kumuuzza iye zomwe iye akuchita; kapena mmodzi wa inu mamembala, chirichonse chomwe inu muli. Ndiye icho nchoti chizibweretsedwa pamaso pa iye. Ngati iye sangati achite izo, ndiye bwerani mudzawauze abusa. Ndiye, iye azimasulidwa kwa mpingo, ndiyeno musiyeni iye akhale monga wachikunja ndi wawamba. Ndiye muwawone Ambuye akapita kukagwira ntchito pa iye. Mukuona, ndi pamene iye amabwerera kwa iyemwini. Ndi pamene iye amapita achokwawa umo. Koma ife timayesa kuzichita izo ifeeni, inu mukudziwa, kuyesera kuchita . . . chirichonse momwe ife tingati tichitire izo, tsopano, ife sitimapambanapo nkomwe.

<sup>88</sup> Tsopano, Melkizedeki uyu, Mfumu ya Salemu, Kalonga, Wansembe wa Wammwambamwambayo, anakomana ndi Abrahamu ndipo anamudalitsa iye. Ndipo anamupatsa Iye zachikhumi zake, Abrahamu anatero. Ndipo Iye anali Mfumu ya Salemu. Ndipo Iye anabweretsa uko mkate ndi vinyo, mgonero, ndipo anapereka izo kwa Abrahamu itatha nkondo, amunawo atagonjetsedwa kale.

<sup>89</sup> Tsopano, “Nkhondo zonse,” monga ine ndinanena, “zimamenyedwera chifukwa cha mfundo.” Tsopano, ngati inu muli ndi kankhondo kakang'ono mu mpingo, iyo iyenera kukhala pa mfundo yoyenera. Inu muyenera kuti muzimenyera chinthu cholondola. Ndipo membala aliyense wa mpingo amayenera kuti azichita zimenezo. Tsopano, kuphunzitsa uku ndi kwa mpingowu. Ndi chomwe ife tiriri nacho pano. Ndi

chomwe ine ndiri kuimira nacho pano. Ndi chomwe Mawu a Mulungu ali a icho, ndi za kwa mpingo.

<sup>90</sup> Musati muzilola chirichonse chiziutchinga mpingo uno. Ngati icho chitero, ndinu olakwa, aliyense wa inu. Ndipo inu, mu mipingo yanu yosiyana, ngati chinachake chikulakwika mu mpingo wanu, ndinu olakwa, chifukwa ndinu oyang'anira a mpingo umenewo. Izo siziri kwa m'busa. Izo siziri kwa gulu la madikoni. Izo ziri kwa inu, inu panokha, kuti mupite kwa m'bale ameneyo ndi kukawona ngati inu mungamuyanjanitse iye. Ngati sichoncho, ndiye mutenge awiri kapena atatu limodzi nanu, ndiye mubwerere. Iye akapanda kuwamva awo; kazineneni izo kwa mpingo. Ndiye iye achotsedwa ku Ufumu wa Mulungu, Mulungu anati, "Ngati inu mumuchotsa iye uko, Ine ndimuchotsa iye Kuno, ngati inu munadutsa mu dongosolo ili." Ndiye Iye atembenezira Mdierekezi kwa iye kuti amukonze. . . kuwonongeka kwa thupi lake. Ndiyeno iye abwerera. Ndiko kulondola. Ndiyo njira yomupangira iye kuti abwerere. Ngati iye ali mwana wa Mulungu, iye abwerera. Ngati iye sali, bw—bwanji, iye azipitirira nazo, ndiyeno Mdierekezi amutumiza iye ku malo ake Amuyaya.

<sup>91</sup> Tsopano, zopangitsa za izo. Ngati inu mungozitengera izo umo chifukwa cha winawake, ndiye izo nzosiyana. Koma, ngati munthuyo ali wolakwa! Ndipo Loti anali atapita uko ndipo anakabwerera mmbuyo, ngakhale iye anali Wachihebri. Iye anapita uko ndipo anali atabwerera mmbuyo. Iye anali mu chisomo, koma iye anali atagwa kuchokera kwa icho. Ndipo pamene iye anapita kwina. . . Ndipo Loti—Loti anali wopulumutsidwa. Musati muziganiza kuti Loti sanali wopulumutsidwa. Iye anali. Chifukwa, nthawi zonse pamene iye anali mu malo olakwikawo, Baibulo limanena, kuti, "Machimo a Sodomu ankausautsa moyo wake wolungamawo pa tsiku." Tsopano, thupi lake linali kuchita chinthu china. Ndipo kodi mathero ake anali chiani? Iye anabweretsa chamanyazi chochuluka. Mkazi wake anasandulika chulu cha mchere. Iye anabereka ana mwa ana ake aakazi. Chotero, inu mukhoza kuwona chamanyazi chomwe izo zinabweretsa, chifukwa iye anali atagwa kuchokera ku chisomo ndipo sanadzibwezeretsere konse iyeyekha kachiwiri. Ndipo Mulungu anachita kumuchotsa iye mu dziko lapansi.

<sup>92</sup> Koma, apobe, iye anali m'bale wakugwa, ndipo Abrahamu anachita zonse zomwe iye akanakhoza kuzichita kuti amubwezeretse iye kachiwiri. Ndipo Mzimu umene unali mwa Abrahamu, unali Mzimu wa Khristu umene uli mu mpingo lero. Ziribe kanthu zomwe m'bale wachita, inu muchita zonse zomwe inu mungathe kuti mumubwezeretse iye mu chiyanjano cha Khristu kachiwiri. Ziribe kanthu zomwe iye wazichita, inu muyesera zolimba.

<sup>93</sup> Tsopano, ife tikufuna kuti tizindikire apa tsopano kachiwiri, pamene ife tikupitirira nalo phunziro ili la Melkizedeki uyu, Wansembe wamkulu uyu wa ku Salemu, ndi mwini wa Miyamba ndi dziko lapansi. Tsopano, pokhala poyamba:

*Wopanda bambo, wopanda amayi, wopanda kochokera, wopanda ngakhale chiyambi cha masiku, ngakhale mathero a moyo; koma anapangidwa monga mwa mawonekedwe a Mwana wa Mulungu; akanali wansembe mopitiriza.*

Tsopano penyani. Iye sanali Mwana wa Mulungu. Iye anali Mulungu wa Mwana. Iye sanali Mwana wa Mulungu, Melkizedeki sanali, koma Iye anali Atate wa Mwana wa Mulungu.

<sup>94</sup> Tsopano, thupi ili lomwe Iye anali nalo, Iye anali atalilenga. Ilo silinachite kubweretsedwa kudzera mwa mkazi. Chotero ndi thupi lolengedwa ilo, Iye sakanatha. . .Thupi lina lomwe Iye anali atalipanga, Iyemwini, kuti adziululiremo Iyemwini.

“Palibe munthu angathe kumuwona Mulungu pa nthawi iliyonse. Mulungu ndi mzimu.” Maso achivundi samawona zinthu zimenezo, kupatula ngati izo zitakhala mu mawonekedwe onga a Lawi la Moto, kapena chirichonse chomwe icho chinali, kapena mu mawonekedwe a chokhalapo chinachake chomwe iwo anachiwona mwa masomphenya. Koma. . .Mulungu amayenera kuti azidziwulula Iyeyekha kupyolera mu njira inayake. Ndipo Mulungu anadziulula Iyeyekha kwa Abrahamu, mwa mawonekedwe a munthu. Iye anadziululira Iyeyekha kwa Mose, mu mawonekedwe a munthu. Iye anadziululira Iyeyekha kwa ana a Israeli, mu mawonekedwe a Lawi la Moto. Iye anadziululira Iyeyekha kwa Yohane Mbatizi, mu mawonekedwe a nkunda. Inu mukuona, Iye anadziululira Iyemwini mu mawonekedwe amenewo.

Pamene Iye anali akudziulula Iyemwini mu mawonekedwe a Munthu, monga Mfumu ya Salemu; ya Yerusalemu; osati ya Yerusalemu wapadziko lapansi, koma Yerusalemu Wakumwamba. Iye anadziululira Iyemwini mu mawonekedwe amenewo. Iye anapangidwa “monga mwa” Mwana wa Mulungu.

<sup>95</sup> Tsopano, Mwana wa Mulungu ankayenera kubwera kudzera mwa mkazi, kuti adzachite kulengedwa kuno; kudzera mu chiberekero cha mkazi, chifukwa kudzera mu chinthu chomwecho inadza imfa.

<sup>96</sup> Ndipo Iye sakanakhoza kubwera kupyolera mu chilengedwe monga Mulungu anachitira pachiyambi. Pamene Mulungu anamupanga munthu pachiyambi, mkazi analibe kanthu kochita nazo izo. Mulungu anangoti, “Siyani pakhale pali,” ndipo munthu anabwera kuchokera ku fumbi. Iye anamuitana iye, popanda mkazi aliyense woti akhale ndi chochita chirichonse kwa izo. Koma, mkazi, iye apo anali mwa mwamuna.

<sup>97</sup> Ndipo Mulungu anamutenga mkazi kuchokera ku mbali ya Adamu. Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndiyeno mkazi anapita nakamubala mwamuna kupyolera mu kugonana. Chotero njira yokha yomwe Mulungu akanakhoza kuchitira. . . Iye sakanati abwere mu fiofane ija. Iye sakanakhoza kubwera ngati Melkizedeki. Iye anayenera kubwera ngati mwamuna, ndipo iye anayenera kubwera kudzera mwa mkazi. “Mbewu yako idzavulaza mutu wa serpenti, ndipo mutu wake udzavulaza chitendene Chako.” Mukumvetsa izi? [“Ameni.”] Mulungu anayenera kubwera kudzera mwa mkazi; ndipo Iye anatero, pamene Iye anadzakhala mu thupi Lake la Mwana Wake, Khristu Yesu. “Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjanitsira dziko kwa Iyemwini. Ndipo Iye anapereka Magazi Ake Omwe ngati nsembe. Ndipo anapereka moyo Wake, kuti kupyolera mu mpita wa imfa, Iye akhoze kukupulumutsirani inu ku Moyo Wamuyaya.

<sup>98</sup> Chotero Mulungu anabwera apo, ndipo Iye anapangidwa “monga mwa” Mwana wa Mulungu. Mukuona? Iye anali Mwamuna wopangidwa *monga* Mwana wa Mulungu. Tsopano, Iye sakanati akhale Mwana wa Mulungu, chifukwa Munthu uyu ndi Wamuyaya.

<sup>99</sup> Mwana wa Mulungu anali ndi chiyambi, Iye anali ndi mathero. Iye anali n—ndi nthawi ya kubadwa Kwake, Iye anali ndi nthawi ya kufa Kwake. Iye anali nazo zonse chiyambi ndi mathero. Iye anali nawo onse atate ndi amake.

<sup>100</sup> Munthu uyu analibe ngakhale bambo kapena amake, chiyambi kapena mathero a nthawi. Koma Iye anapangidwa, Munthu uyu, Melkizedeki, anapangidwa *monga* Mwana wa Mulungu.

<sup>101</sup> Tsopano, Mwana wa Mulungu, pamene Iye anabwera mu dziko, mu mawonekedwe a mkazi, kudzera mwa mkazi, mu mawonekedwe a mwamuna; ndipo anaphedwa, anauka kachiwiri pa tsiku lachitatu, anauka kwa chirungamitso chathu, tsopano Iye akukhalapo kwanthawizonse. Ndipo utali wonse pomwe thupi limenelo likukhalapo, ife tikukhalapo nafenso. Ndipo chifukwa Iye anauka kuchokera mu fumbi, ife tidzaukitsidwa mwa mafananidwe Ake. Ndi imeneyo nkhani ya Uthenga. Lodala likhale Dzina la Ambuye. Osati Angelo, osati zinthu zauzimu, osati mulu wa nthenga kuti tiziuluka uluka, koma amuna ndi akazi, ameni, titaima mu mafananidwe Ake. Inde, bwana.

<sup>102</sup> Monga ine mowirikiza ndakhala ndikunena izi, ine ndikunena izo kachiwiri pano pa nthawi ino. Izo zikuwoneka zoyenera. Ine ndinali kupesa, pafupi lisanu ili kapena tsitsi lisanu ndi limodzi lomwe ine ndatsala nalo. Ndipo akazi anga anati, “Billy, iwe ukuyamba dazi.”

<sup>103</sup> Ine ndinati, “Koma ine sindinataye limodzi la ilo.”

104 Iye anati, “Liri kuti ilo?”

105 Ine ndinati, “Ndiuze ine komwe ilo linali ine ndisanakhale nalo ilo, ine ndikuuza iwe komwe ilo likundidikirira ine.” Ndiko kulondola.

106 Ine poyamba ndinali monga—womenya, wankhonya. Ine ndinali wamphamvu ndi wamkulu. Ndipo ine ndinkamverera, ngati inu mungaike tchalitchi ichi pa nsana wanga, ine nkukhoza kumayenda nacho pa msewu icho. Ine ndikukuuzani inu, pamene ine ndimauka mmawa uliwonse tsopano, ine ndimazindikira kuti pali zaka forte ndi chinachake zadutsa. Mukuona? Ine sindiri chomwe ine ndinalicho. Ine ndikulephera, tsiku lililonse. Pamene ine ndiyang’ana pa manja anga ndi kuganiza, “Taona apa. Chabwino, ine ndikukhala munthu wokalamba.” Ine ndikayang’ana pa mapewa anga. Ine ndikuwona kuti ine ndaonjezera kulemera kochulukika. Ine ndinkavala lamba pa twente eyiti. Ine ndikuvala sate tsopano. Mukuona, ine ndikukhala wokalamba, kunenepa, kuyamba kuthapo.

107 Ndi chiani icho? Ine ndikumadya chinthu chomwecho ine ndinali kuchidya. Ine ndikukhala moyo waukhondopo ndi mwabwinopo kuposa momwe ine ndinali kukhalira moyo, chinthu chomwecho. Koma Mulungu anaika nthawi kwa ine, ndipo ine ndiyenera kuilandira iyo. Koma ganizo lodala ndilo, kuti, pa tsiku limenelo, Iye adzandidzutsa ine kachiwiri. Ndipo chirichonse chomwe ine ndinali pamene ine ndinali wausinkhu wa zaka twente-faifi, ine ndidzakhala kachiwiri kwanthawizonse. Ameni. Ndi inu apo. Nchiani cha ukalamba chomwe chikundivuta ine? Ine ndidzamugonjetsa Mdierekezi pa izo kwa zaka ndi zaka, podziwa ichi, kuti ine ndikumukhulupirira Iye. Kadanga kakang’ono aka ndi kanthu, kakang’ono kakafupi, mulimonse. Ngati ife tikadakhala kokha matwente awiri ndi teni, usinkhu wa zaka sevente, nthawi yathu yolonjezedwa, nchiani—chimenecho nchiani koma umphawi ndi zowawa? Nchiani chimenecho? Kodi inu mungasinthanitse nyumba ya tizirombo iyi mmalo mwa chinthu chaulemerero icho kutaliko?

108 Bwanji, lodala likhale Dzina la Ambuye! Chinachake mkati mwa ine chinakomana naye Melkizedeki uyo tsiku lina, ndipo Iye anayankhula mtendere kwa ine ndipo Iye anandipatsa ine Moyo Wamuyaya. Ndipo moyo uno sukutanthauza kanthu koma kachisi woti ndizilalikiriramo Uthenga. Ine ndikunena izi ndi kudzipereka konse, ndi ma Baibulo awiri awa ali chitsegulire patsogolo panga. Ngati Mulungu wanga akanati athane nane mkulalikira Uthenga, ndi kuti ine sindingamuchitirensa kanthu Iye, ana anga atakhala oti akula mokwanira kuti akhoza kumadzisamalira mwaokha, ndipo Iye akufuna kuti anditenge ine pakali pano, “Ameni,” izo zingakhazikitse icho. Inde, bwana.

109 Kodi zikupangitsa kusiyana kwanji ngati ine ndiri eyite kapena ngati ine ndiri twente? Ine ndiri kokha kuno kwa chinthu chimodzi: kuti ndiziwatumikira Ambuye. Ndizo zonse. Ngati ine ndingakhoze kumalalikirabe Uthenga monga ine ndikuchitira panomu, pamene ine ndiri eyite, kodi izo zikupanga kusiyana kwanji ngati ine ndiri sate kapena eyite? Pali amuna ambiri ali usinkhu wa zaka eyite usikuuno. Ndipo alipo ana ambiri ati afe, pamene bambo wausinkhu wa zaka eyite ati akhale moyo moposa wina aliyense wa iwo. Kodi izo zingapange kusiyana kwanji? Ndi zokupangitsa zako, mfundo zako, ndipo ife tiri kuno kuti tiziwatumikira Ambuye Yesu. Ndizo zonse.

110 Podziwa ichi, kuti, “Moyo uno ndi nthunzi womwe munthu amayankhula za iwo; kuti kamodzi unalipo, ndiyeno iwo palibe.” Koma ngati ife tiri nawo Moyo Wamuyaya, Mulungu walonjeza kuti Iye adzatidzutsa ife kachiwiri. Ndipo ife tidzakadya mgonero limodzi ndi Iye pamene masiku adzatha, ndi pamene Iye adzati, “Lowani mu zisangalalo za Ambuye, zomwe zinakonzedwera kwa inu kuchokera pa maziko a dziko.”

111 Ndiye ndi kusiyana kotani zomwe zingapange kuno, kaya ife tiri nacho china chirichonse kapena ife tiribe? Kaya ndife aang’ono kapena ndife achikulire, kodi ndi kusiyana kwanji komwe izo zimapanga? Chinthu chofunikira, kodi inu mwakonzeka kukomana naye Iye? Kodi inu mukumukonda Iye? Kodi inu mungamamutumikire Iye? Kodi inu mwadzigulitsa nkutha ku zinthu za mdziko? Kodi inu mwakomana naye Melkizedeki kuchokera pomwe nkhondo inatha?

112 Dalitsani Mulungu! Pafupi usinkhu wa zaka twente wani, ine ndinali, ndipo tsiku lina ine ndinali ndi nkhondo ndi *ichi*, *icho*, ndi *china*. Ine sindinkatha kudziwa ngati ine ndimafuna kuti ndikhale wankhonya, kapena ngati ine ndimafuna kuti ndikhale mlenje, kapena msaki, chomwe ine ndinkafuna kuti ndikhale. Koma ine ndinakomana naye Melkizedeki, ndipo Iye anandipatsa ine mgonero, ndipo kuchokera pamenepo ndiye izo zinakhazikitsidwa kwanthawizonse. Aleluya! Ine ndapita ku mbali Yake. Ine ndakhala ndikusangalala pa njirayi. Ndipo pamene izo zidzafika kumathero a njirayi, ndi imfa ikundiayang’ana ine mu nkhope; momwe ine ndikumverera pano, ine sindidzaiwopa konse iyo. Ine ndidzayenda, ndikufuna kuti ndidzayende mpaka mu nkhope ya iyo, podziwa ichi, kuti ine ndikumudziwa Iye yemwe anapanga lonjezo, ndiko kulondola, kuti ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiukitsiro Chake. Pamene Iye adzaitana kuchokera pakati pa akufa, ine ndidzatuluka kuchokera pakati pawo. Ndiko kulondola, kumudziwa Iye mu mphamvu ya chiukitsiro Chake. Ndi kusiyana kotani komwe izo zikupanga, kaya ndine wamkulu kapena ndine wamng’ono? Kaya ndine wochepa kapena ndine wamkulu? Kaya ine ndakhuta kapena ndine wanjala? Kaya ine ndiri nawo malo oti ndigonepo kapena ine ndiribe?



113 “Mbalame ziri ndi zisa, ndipo nkhandwe ziri ndi mphanga, koma Mwana wa munthu alibe malo oti ayikepo mutu Wake,” koma Iye anali Mfumu ya Ulemerero.

114 Ife ndife mafumu ndi ansembe usikuuno. Ndi kusiyana kwanji komwe izo zikupanga kaya ife tiri nazo kapena ife tiribe? Bola ngati ife tiri naye Mulungu, ife tiri oposa agonjetsi. Ife tiri oposa agonjetsi. Ife tikukhala mu Kukhalapo kwa Mulungu, mu chiyanjano cha Mzimu Woyera, kumadya mgonero Wauzimu kuchokera mmanja a Iye yemwe anachitira umboni, “Ine ndinali Iye yemwe anali wakufa, ndi wamoyo kachiwiri, ndipo ndiri wamoyo kwanthawizonse.” Tikukhala limodzi mu malo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu. O lodala likhale Dzina Lake loyera. Ndi kusiyana kotani komwe izo zikupanga?

Hema kapena khumbi, ndisamalirenji ine?  
Iwo akundimangira ine nyumba yachifumu  
Kumeneko!  
Ya miyala yodula ndi madaimondi, ndi siliva  
ndi golide,  
Mosungira mwake ndi modzaza, Iye ali ndi  
chuma chosasimbika.

115 Ine ndinakomana naye Iye tsiku lina pamene ine ndinkabwera kuchokera ku nkhondo. Ine ndinaika zikho zanga pansi. Ine sindinamenyepo nkhondo kuchokera pamenepo; Iye amandimenyera izo ine. Ine ndimangopuma pa lonjezo Lake, podziwa ichi, kuti ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiukitsiro Chake. Ndizo zonse zomwe zikufunika. Ndi chianinso chomwe chikufunikira?

116 Kodi ife tingachite chiani? “Kodi kutenga lingaliro kungawonjezere muyezo umodzi kwa usinkhu wanu? Chifukwa chiyani inu mukusamala ngati tsitsi lanu liri lopindika, kapena ngati inu muli nalo lirilonse kapena ayi? Ndi kusiyana kotani komwe izo zikupanga? Ngati inu muli wokalamba, ngati inu muli waimvi, ngati inu muli wokugwa-mapewa, ngati inu simuli, ndi kusiyana kotani komwe izo zikupanga? Amen. Izo ziri kwa kanthawi kokha, kadanga kakang’ono, koma Ilo ndi la nthawi za nthawi. Ndipo pamene ma ayoni a nthawi akupitirira, pamene mibadwo ikupitirira, inu simudzasintha konse, ndi kupita kudutsa mu mibadwo Yake yosatha Yamuyaya. Ndi kusiyana kotani komwe izo zikupanga?”

117 Ndine wokondwa kwambiri ine ndinakomana naye Iye. Ndine wokondwa kwambiri Iye anandipatsa ine mgonero, tsiku lina, Melkizedeki yemwe uja yemwe anakomana naye Abrahamu akubwera kuchokera kokawapha mafumu. Ndithudi. “Mulungu Wakumwamba,” *El Elyon*; “INE NDINE” wamkulu, osati ine ndinali; INE NDINE, tensi yatsopano. “Ndipo Iye anamudalitsa iye.”

118 Mvetserani apa mopitiriza pang'ono pokha, chotero ife tikhoze kupeza phunzirolo moyandikira pang'ono limodzi. Tsopano ndime ya 4.

*Tsopano lingalirani momwe munthu uyu analiri wamkulu, . . .*

Ine ndikungoganiza izo, nanenso. “Lingalirani momwe Munthu uyu analiri wamkulu.” Iye ali wopitirira pa Mwana wa Mulungu. Mwana wa Mulungu anali ndi abambo ndi amake; Iye analibe. Mwana wa Mulungu anali ndi chiyambi cha nthawi ndi mathero a nthawi; Iye analibe. Anali ndani ameneyo? Ameneyo anali Atate wa Mwana. Ndi Yemwe iye anali.

*. . . lingalirani momwe munthu uyu analiri wamkulu, mpaka . . . ngakhale mbadwa Abrahamu anapereka chakhumi cha zofunkha zake zonse.*

119 Tsopano mvetserani mwacheru.

*Ndipo indetu iwo omwe ali a ana a Levi, omwe amalandira udindo wa unsembe, ali nalo . . . lamulo loti azitenga zachikhumi za anthu molingana ndi lamulo, izo ndizo, za abale awo, ngakhale iwo anabwera kuchokera mchiuno mwa Abrahamu:*

120 Tsopano penyani ichi ngati inu mukufuna kuti muwone chinachake.

*Koma iye yemwe kuchokera kwake sikuli kupitirizidwa pakuti . . . kuchokera kwa iwo akulandira chakhumi cha Abrahamu, ndipo anamudalitsa iye yemwe anali nalo lonjezo.*

121 Abrahamu anali nalo lonjezo, ndipo Munthu uyu anamudalitsa Abrahamu yemwe anali ndi lonjezo. Anali ndani uyu? Ana a Levi amapereka zachikhumi kwa abale awo kapena . . . Abale awo amapereka zachikhumi kwa iwo. Iwo anali nalo lamulo la Ambuye kuti azitenga zachikhumi za zomwe abale awo ankapanga, kuti azikhalira moyo, chifukwa iwo anali aunsembe. Tsopano, izo zikusiya kunja unsembe wa Melkizedeki, momwe inu mukuyankhulira za izo, apo pomwe. Ndiko kulondola. Koma Munthu uyu . . . Ngakhale iye yemwe anali nalo lonjezo, munthu wamkulukulu pa dziko lapansi, Abrahamu, anakomana naye Munthu uyu ndipo anapereka zachikhumi kwa Iye. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Iye anayenera kukhala ali wamkulupo.

122 Mvetserani.

*Ndipo popanda kutsutsana kulikonse wamng'ono amadalitsidwa ndi wamkulu.*

Ndithudi. Penyani Yemwe Iye ali.

*Ndipo kuno amuna omwe amafa amalandira zachikhumi; . . .*

Uwo ndiwo unsembe wa dongosolo la ansembe ndi alaliki, ndi ena otero. Amuna omwe amalandira chakhumi, amafa. Mukuona?

*...koma kuno iye akulandira izo, kwa iye yemwe zikuchitiridwa umboni kuti iye alimoyo.*

<sup>123</sup> Kodi munthu akanati azitengerenji zakhumi, ngati iye anali chirichonse...Ngati iye sanabadwe konse, ndi kuti sadzafa konse, ndipo analipo kuchokera kuchiyambi mpaka kumapeto, n—ndipo analibe konse bambo kapena amake, kapena kochokera, ndipo ali mwini wake wa Miyamba yonse ndi dziko lapansi ndi zonse ziri mmenemo, nchifukwa chiani iye akanati azitenga chakhumi? Chifukwa chiani anamufunsa Abrahamu kuti apereke zachikhumi? Inu mukuona chomwe chinthu chosamalitsa icho chiri kuti uzipereka zachikhumi? Kupereka chachikhumi ndi kolondola. Mkhristu aliyense ndi wokakamizidwa kuti azipereka chachikhumi. Ndiko kulondola. Sizinayambe zasinthidwa konse.

<sup>124</sup> Tsopano:

*Ndipo monga ine ndinganene chotero, Levi nayenso, yemwe ankalandira chachikhumi, anapereka zachikhumi mwa Abrahamu.*

<sup>125</sup> Tsopano, o, apa pali chinachake.

*Pakuti iye anali akadali apabe mu ziuno za atate ake, pamene Melkizedeki anakomana naye iye.*

<sup>126</sup> Chiani, Levi? Abrahamu anali agogo-agogo-a amuna a Levi. Ndipo Baibulo linanena apa, kuti, “Levi anapereka zachikhumi pamene iye anali mu ziuno za Abrahamu.” Mibadwo inai iye asanabwere konse pa dziko lapansi, iye anali akupereka zachikhumi kwa Melkizedeki. Lodala likhale Dzina la Ambuye!

<sup>127</sup> Ndiye, inu omwe simungathe kukhulupirira mu kukonzedweratu kudzozedweratu kusanachitike; ndipo apa, timbadwo tinai Levi asanabwere konse kuchokera mu ziuno za Abrahamu, anali akupereka zachikhumi kwa Melkizedeki. Ndikukhumba ife tikadakhala nayo nthawi yoti tiziyendetse izi kudutsa mu Lemba.

<sup>128</sup> Ngati inu mungazitengere izo ku Yeremiah 1:4, Mulungu anati, “Ine ndinakudziwa iwe usanawumbidwe nkomwe mu chiberekero cha amayi ako. Ndipo ine ndinakuyeretsa iwe ndi kukudzozeratu iwe ukhale mneneri kwa mafuko.” Ndiye iwe unganene chiani kuti iwe unachichita? Ine ndinganene chiani kuti ine ndinachichita? Ndi Mulungu yemwe amasonyeza chifundo. Mulungu anatidziwa ife asanaikidwe maziko a dziko.

<sup>129</sup> Iye Sali kulolela kuti wina awonongeke. Ndithudi ayi. Koma ngati Iye ali Mulungu, Iye anadziwa yemwe akanati adzapulumutsidwe ndi yemwe sakanati adzapulumutsidwe, kapena Iye sankadziwa kalikonse. Ngati Iye sankadziwa...

Ngati iye sankadziwa yemwe akanati adzakhale mu Mkwatulo, dziko lisanapangidwe konse, ndiye Iye si Mulungu. Ngati Iye ali wopandamalire, Iye bwezi. . . Iye ankadziwa utitiri uliwonse, ntchentche iliyonse, nsabwe iliyonse, phata aliyense, zomwe zikanati zidzakhale konse pa dziko lapansi ilo lisanawumbidwe nkomwe. Ndiko kulondola. Iye anadziwa zinthu zonse. Asanaikidwe maziko a dziko, Iye anadziwa ife. Baibulo linanena, kuti, “Iye anadziwa ife ndipo anatikonzeratu ife.”

<sup>130</sup> Tiyeni tizikhazikitse izi kamodzi kokha. Tiyeni tibwerere ku Aefeso, mutu woyamba. Mutu wa 5-. . . Mutu woyamba wa Aefeso, mphindi yokha. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge apa miniti yokha chotero, kuti inu mukhoze kumvetsa kwenikweni kuti si chinachake basi chomwe ine ndikuyesera kuti ndikuuzeni inu. Ndi chinachake chomwe Mulungu akuyesera kuti akuuzeni inu. Mukuona? Tsopano mveterani kwa izi, mwatcheru kwenikweni, mutu woyamba wa Aefeso.

*Paulo, mtumwi wa Yesu Khristu mwa chifuniro cha Mulungu, . . .*

Munthu yemweyo amene analemba kalata ya Ahebri, akulemba kalata iyi.

*. . .kwa oyera . . .*

Izi si za kwa osakhulupirira, koma kwa oyera, oyeretse-. . . oyerawo.

*. . .omwe ali mu Efeso, ndi kwa okhulupirika mwa Khristu Yesu:*

*Chisomo chikhale kwa inu, ndi mtendere, zochokera kwa Mulungu Atate athu, ndi kuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu.*

*Wodala akhale Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Khristu, yemwe watidalitsa ife ndi madalitso onse auzimu mu malo ammwambamwamba . . .*

“Molingana monga Iye. . .” Tsopano, mveterani mwatcheru tsopano, ndime ya 4.

*Molingana monga iye anatisankha ife mwa iye asanakhazikitsidwe maziko a dziko, . . .*

Kodi “ife” ndi ndani apo? Mpingo.

*. . .iye anatisankha ife mwa iye (Khristu) asanakhazikitsidwe maziko, dziko lapansi, kuti ife tikhale tiri oyera ndi opanda chilema pamaso pa iye mu chikondi:*

*Atatikonzeratu ife ku kukhazikitsidwa kwa ana mwa Yesu Khristu kwa iyemwini, molingana ndi kukondweretsedwa kwake komwe kwa chifuniro chake,*

<sup>131</sup> Nndani anazichita izo? Mulungu anazichita izo. Mulungu ankadziwa kuchokera ku chiyambi yemwe akanati

adzapulumsidwe ndi yemwe sakanati adzapulumutsidwe. Ndithudi. Iye sanali kulolera kuti wina aliyense awonongeke. Koma Iye sanamutumize Yesu kuno kuti adzangowona ngati i—inu mungadzachite monga ngati, “Chabwino, Yesu wosauka, ine ndikumumvera chisoni Iye. Mwinamwake ine ndibwino kuti ndipulumutsidwe ndi kutsimikizira izo.” Ayi, bwana.

<sup>132</sup> Mulungu ankadziwa pachiyambi yemwe akanati ndi yemwe sakanadzati. Chotero, potero, Iye ankadziwa kuti ena akanadzatero, chotero Iye anamutumiza Yesu kuti adzapange chitetezero kwa iwo omwe Iye anawadziwiratu. “Pakuti iwo omwe Iye anawadziwiratu, Iye anawaitana. Ndipo iwo omwe Iye wawaitana, Iye anawalungamitsa. Ndipo iwo omwe Iye wawalungamitsa, Iye anawapatsa (tensi yakale) ulemerero.” Ndi inu apo.

<sup>133</sup> Chotero si inuyo omwe mumadzisunga nokha, ndi chisomo cha Mulungu chomwe chimakusungani inu. Inu simunadzipulumutse nokha, kapena palibe kanthu komwe inu munachita koti muyenere kuti mupulumutsidwe. Ndi chisomo cha Mulungu chomwe chinakupulumutsani inu. Chisomo cha Mulungu chinakuitanani inu. Kudziwiratu kwa Mulungu kunakudziwani inu. Iye ankadziwa kuti inu mukanadzakhala mu mpingo uno usikuuno, maziko a dziko asanaikidwe konse, ngati Iye ali wopandamalire. Ngati Iye sali, Iye si Mulungu. Ngati Iye anali kudziwa zinthu zonse, Iye anali Mulungu. Ngati Iye anali kudziwa zinthu zonse, Iye sanali Mulungu. Ngati Iye ali Mulungu Wamphamvuzonse, Iye akhoza kuchita zinthu zonse. Ngati Iye sangathe kuchita zinthu zonse, Iye si Mulungu Wamphamvuzonse. Ndi inu apo.

<sup>134</sup> Chotero inu munganene bwanji kuti ndi chinachake chomwe inu mungathe kuchita? Palibe chomwe inu mungathe kuchita. Ndi chisomo cha kukonda kwa Mulungu kwa inu, kuti inu muli ngakhale pano. Palibe kanthu komwe inu mukanati muchite, Mulungu anakuitanani inu mwa chisomo Chake; inu munamvetsera, munamva, munavomereza.

<sup>135</sup> “Chabwino,” inu mukuti, “M’bale Branham, izo zikupangitsa kumasuka kwambiri.” Ndithudi zikutero. Ndinu mfulu. “Chabwino, munthu ameneyo akhoza kumachita chirichonse chimene iye akufuna kuchichita.” Mwamtheradi. Ine nthawizonse ndimachita zomwe ine ndimafuna kuzichita. Koma ngati iwe uli Mkhristu, iwe sumafuna kuti uzichita zolakwika.

<sup>136</sup> Pali msungwana wamng’ono wachikulire wakhala kumbuyo uko usikuuno, mkazi wanga. Ine ndimamukonda iye ndi zonse zomwe ziri mwa ine. Ndipo ngati ine ndikanamadziwa kuti ine ndikanatha kumayendayenda ndi mkazi wina ndi kudutsa nazo izo, ndi kupita kukamuza iye, ndi kuti, “Meda, ine ndinachita cholakwika,” kodi inu mukuganiza kuti ine ndikanachita izo?

Ngati ine ndimamukonda iye moyenera, ine sindingati ndichite izo. Ndiko kulondola.

<sup>137</sup> Tsopano, bwanji ngati ine ndikanati, “O, ine sindingathe kuchita izo. Poti, ine ndikuuzeni inu chifukwa chake. Iye angati andisiye ine chikwati, ndipo ine ndiri . . . O, ndine mlaliki. Mukuona chomwe izo zingati zichite? Izo zingandichotsetse ine pa guwa, ngati iye angati andisiye ine chikwati. ‘Mwamuna wosudzulidwa, o!’ ine ndiri ndi ana atatu; ine sindingathe kuganiza za izo. Koma, mnyamata, ine . . .”? Chabwino, ngati umo muli momwe izo ziriri, inu mukadali amwamalamulo. Si mwa maziko a malamulo omwe ine ndinamukwatirira iye. Si maziko a malamulo omwe amandipangitsa ine kuti ndizikhala moyo woona kwa iye. Ndi chifukwa kuti ine ndimamukonda iye. Ine sindimasowa kuti ndichite chirichonse. Ine ndimachita izo mwakufuna chifukwa ndi nkhani yachikondi. Ndipo ngati inu mukuwakonda akazi anu, inu muzichita chinthu chomwecho.

<sup>138</sup> Ndipo ngati inu mukumukonda mkazi wanu monga choncho, ndi chikondi cha *fileo*, inu mukuyenera kumachita chiani kwa Khristu ndi chikondi cha *agapao*, chomwe chiri kuchulukitsa kamilioni mwamphamvupo, ngati inu mukumukonda kwenikweni Mulungu? Ngati ine ndikanadziwa usikuuno kuti ine ndingathe kupita ndi kumakaledzera, ngati ine ndikanadziwa usikuuno kuti ine ndikhoza kumayenda yenda ndi kukhala wopanda khalidwe, ngati ine ndikanadziwa, usikuuno; ngati izo zikanakhala ngakhale mu mtima mwanga kuti ndizichita chomwecho, ndipo ine ndikanapita ndi kukazichita izo, ndikudziwa kuti Iye akanati andikhululukire ine, ine sindikanati ndichite izo. Ine ndimaganza mochuluka kwambiri za Iye. Ine ndimamukonda Iye. Zedi. Ndithudi.

<sup>139</sup> Ndicho chifukwa ine sindikanati ndigulitse zondichitikira zanga kwa chipembedzo chirichonse, (ayi, bwana), osati Assemblies of God, osati mpingo wa Mulungu, osati Pilgrim Holiness, Methodisti, Baptisti, Presbateria, Katolika. Ine sindikanati nditenge chirichonse chomwe chikanati chiperekedwe, kwa chondichitikira ichi. Chifukwa, icho sichimabwera konse ndi munthu. Icho chinabwera ndi Mulungu. Ayi, bwana. Ine sindikanati ndigulitse ufulu wakubadwa wanga chifukwa cha roke-n-rolo iliyonse ya Elvis Presley, kapena chifukwa cha mndandanda wake wa Akatolika, kapena Makadilaki ake, kapena mamilioni dola ake, ndi zina zotero, zomwe iye amazipeza mwezi uliwonse. Ayi, bwana. Ine ndimamukonda Iye. Ndipo ngati ine . . . Utali wonse womwe ine ndikumukonda Iye monga choncho, ine ndizikhala moona kwa Iye. Ndipo ngati Mulungu wandiitana ine ndipo wandisankha ine, Iye waika chinachake mkati mwanga, ndipo ndikumukonda Iye.

<sup>140</sup> Ine ndikumukumbukira Bambo Isler. Inu nonse mukumudziwa iye, pafupi nonse inu. Iye ankabwera kuno,

nduna ya dziko ya dera la Indiana; ankabwera kuno, kumasewera gitara yawo. Pamene mwana wanga anafa, mkazi wanga anali atafa, ndipo onse awo atagona kumanda uko. Ndipo ine ndinali ndikudutsa mu msewu, manja anga ali kunkhongo, ndikulira. Iye anadumpha kuchokera mu galimoto yake, yaing'ono yakaleyo, ndipo anabwera nkudzaika nkono wake mozungulitsa pa ine, anati, "Billy, ine ndikufuna kuti ndikufunse iwe funso." Anati, "Ine ndakumva iwe ukulalikira mpaka iwe umakhala pang'ono kuti ugwere pa guwa. Ndakumva iwe pa ngodya za msewu ndi chirichonse, ukufuulira mmalo mwa Khristu." Anati, "Tsopano Iye watenga abambo ako. Iye wamtenga mng'ono wako. Wakulanda iwo onse, ndipo iwo anafera mmikono mwako. Apo iye anafa. Mkazi wako anafa, atagwira manja ako. Ndipo mwana wako anafa, ndi iwe ukuitanira pa Iye kuti akuthandize iwe. Ndipo Iye anatembenuzira nsana Wake pa iwe. Kodi iwe ukuganiza chiani za Iye."

<sup>141</sup> Ine ndinati, "Ine ndikumukonda Iye ndi zonse zomwe ziri mwa ine. Ngati Iye angati anditumize ine ku gehena, ine ndizimukondabe Iye." Iye ndi wolungama. Ine sindikunena izo; zaka twente-sikisi zatsimikizira izo. Ndiko kulondola.

<sup>142</sup> Ngati inu mukumukonda Iye! Osati ntchito, yoti, "Ine sindingathe *izi*, ndipo ine sindingathe kuchita *izo*." Inu mukumukonda Iye mochuluka kwambiri kuti muzichita izo, chifukwa Iye anakusankhani inu. Inu simunamusankhe konse Iye. Iye anakusankhani inu.

<sup>143</sup> Inu munati, "Ine ndinkawafunafuna Ambuye, ndi kuwafunafuna Ambuye."

"Palibe munthu amamufunafuna Mulungu." Ndi Mulungu, amamufunafuna munthu. Inu mukhoza kumafunafuna kokondera kwa Iye, koma Mulungu ayenera kuti asinthe chikhalidwe chanu inu musanati mumufunefune konse Iye. Chifukwa, ndinu wochimwa, ndinu nkhumba. Ndiko kulondola.

<sup>144</sup> Ndipo ena a inu anthu mumapita ku mpingo ndi kumakhaliira moyo umembala wanu wokha, kumapita kunja uko kumakachita chirichonse mu dziko, ndiyeno nkumabwererabe nkuti, "Eya, ndine wa mu mpingo." Chabwino izo ziri kutali kuti mungakhale wa Mulungu. Ndithudi. Ine sindiri. . . Koma, inu mukuona, anthu akamachita izo, inu mukhoza kudziwa. O, iwo ndi mamembala abwino a mpingo. Izo nzoona. Inu mukhoza kukhalabe membala wa mpingo ndi kumachita zinthu zimenezo, koma inu simungakhoze kukhala Mkhristu ndi kumachita zimenezo.

<sup>145</sup> Monga ine ndinanenera, mmawa uja, "Khwangwala wokalamba, ngati panayamba pakhala wachinyengo, ndi khwangwala." Ndiko kulondola. Iye ndi nkunda zinali mu chombo chimodzi, zinali pa chisa chimodzi. Ndipo khwangwala

wakolambayo anakhutitsidwa pamene iye anamasulidwa, ndipo anatulukwa mu Mpingo umenewo, kuti iye akanatha kupita kunja uko ndi kukakhala pa nyama imodzi yakufa ndi “kowo, kowo,” ndi kudya pa *izi*, kudya pa kavalo, ndi kudya pa ng’ombe, ndi chirichonse chomwe chinali, iye anali kukhutitsidwa. Koma pamene Nowa anaimasula nkhunda, iyo siimatha kupeza poti iteretse mphondero za mapazi ake. Iyo inali ndi ufulu wochuluka mofanana kuti itere pa nyama zakufa monga khwangwala ankachitira, koma izo zinali zikhaliidwe ziwiri zosiyana. Wina wa izo, anali nkhunda, pa kuyamba pomwe. Iye anali khwangwala, pa kuyamba pomwe.

<sup>146</sup> Koma, ngati inu mungazindikire, khwangwala wokolambayo angathe kukhala kuno pa nyama yovunda ndi kumaidya, theka la tsiku. Nkhunda ikhoza kukhala mmunda wa tirigu ndi kumamudya, theka la tsiku. Ndipo khwangwala akhoza kuulukira uko komwe ndi kukadya chakudya cha nkhunda, mochuluka momwe iye akufunira kutero. Iye akhoza kudya tirigu wochuluka basi monga khwangwala angadyere...kapena monga nkhunda ingadyere. Koma iye, khwangwala, akhoza kudya chakudya cha nkhunda, koma nkhunda siingakhoze kudya chakudya cha khwangwala. Ndiko kulondola.

<sup>147</sup> Chotero, wachinyengo wokolamba akhoza kubwera mu mpingo, ndi kumasangalala ndi kufuula ndi kumawatamanda Ambuye, ndi kumapitirira nazo monga choncho, ndi kubwereranso kumene ndi kumakasangalala nazo zinthu za mdziko. Koma Mkhristu wobadwa-kachiwiri sangathe kuchita izo, chifukwa chikondi cha Mulungu chimamukakamizira iye ku malo oterowo okuti iye sangathe kuzichita izo.

<sup>148</sup> Chotero ngati inu mwangokhala Mkhristu pojowina mpingo, ndi kusiya kuchita *izi* ndi *izo*, ndipo chikhumbo chomwecho chiri mwa inu, inu mukusowa kumizidwa kwina. Ndizo ndendende kulondola.

<sup>149</sup> Ndipo inu akazi omwe mungamavale zazing’ono izo... zazifupi, ndi kupita pa msewu pomwe kuno, ndiyeno nkumadzitcha nokha “wokhulupirira.” Ndinu wokhulupirira, koma ndinu chitsanzo chosauka cha wina, mwinamwake. Ngati inu mukadakhala naye kwenikweni Khristu mu mtima mwanu, inu simukanati muzilingalira za zinthu zotero monga izo. Ine sindikusamala zomwe akazi ena onse amachita, ndi asungwana ena onse zomwe amachita, inu mukadakhala muli wosiyana, chifukwa inu mumamukonda Khristu mochuluka kwambiri.

<sup>150</sup> Ine ndinkayankhula kwa mkazi tsiku lina, mu nyumba, ndipo iye anaponyera manja ake mmwamba monga *chonchi*, anati, “Abusa a Branham, ine ndiri pafupifupi wamaliseche, muno mnyumba mwanga. Ine ndikuyenda yenda.”



<sup>151</sup> Ine ndinaganiza, “Manyazi pa iwe.” Mnyumba mwanu momwe, ine sindikusamala komwe inu muli. Ndiko kulondola. Zivalani ndi kumachita monga mkazi, monga dona ayenera kumachitira. Manyazi pa inu. Koma inu mumasunga. . . Ndipo Baibulo linati, “Ngati inu mukuzikonda zinthu zimenezo, zinthu za mdziko, chikondi cha Khristu sichiri nkomwe mwa inu.” Ndipo ngati inu mumawakonda Ambuye, basi ndi mtima wanu wonse, ndi solo yanu yonse, ndi malingaliro anu onse, muziika tinthu tating’ono tonyansa, tauve ito kutali ndi inu. Ndiko kulondola.

<sup>152</sup> Ndipo inu madikoni, ndi inu ena kuno, omwe mumayendayenda mu msewu kuno, ndi kumapotola khosi lanu ndi kumayang’ana pa aliyense wa akazi amenewo. Manyazi pa inu; ndipo nkumadzitcha nokha “ana aamuna a Mulungu.” Ine ndikudziwa kuti izo zikuwawula, koma kulibwino kuti muwawulidwe apo kuposa kuti mudzawotchedwe kwanthawizonse uko. Chotero ngati inu mumachita zinthu zimenezo. . . Tsopano, inu simungachitire mwina ngati mkazi akuyenda mu msewu, atavala mwatheka. Inu, ngati inu mukuyang’ana, ndinu woti mumuwona iye, koma inu mukhoza kupotoloza mutu wanu. Baibulo linati, “Aliyense yemwe ayang’ana pa mkazi kuti amusilire iye, wachita chigololo ndi iye kale mu mtima mwake.”

<sup>153</sup> Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, mlongo wokonededwa, inu mupita kukayankha. Ine sindikusamala, inu mukhoza kukhala wangwirowo basi ngati kakombo. Inu mukhoza kukhala kuti simunayambe mwachitapo kwenikweni tchimo la mtundu umenewo, tchimo la makhalidwe oipa, mu moyo wanu. Koma ngati inu mumavala monga chomwecho, inu mudzakayankha pa chiweruzo chifukwa chochita chigololo ndi mwamuna aliyense yemwe ayang’ana pa inu. Baibulo linatero. Ndi kumayenda pansu mu msewu, wolakwa nndani, mwamunayo? Ayi, bwana. Inu muli. Inu munadziwonetsa nokha mwanjira imeneyo.

<sup>154</sup> Mkazi ali nawo malo aakulu. Iwo ndi opatulika, abwino, malo odabwitsa. Koma iye ayenera azidzisunga yekha mwanjira imeneyo, kuti azigwira udindo wake momwe iye ayenera, monga mayi, monga mkazi ndi waukazi. Pamene ukazi usweka, fupa la nsana wa fuko lililonse lasweka. Ndipo ndicho chifukwa, lero, fuko lathu lawonongeka, ndi chifukwa cha kupanda makhalidwe kwa akazi athu. Ndiko kulondola ndendende. Zedi. Ndi kuvunda pakati pathu, komwe kukuliswa ilo.

<sup>155</sup> Chomwe inu mukusowa ndi kukomana naye Melkizedeki uyu nthawi ina. Ameni. Nkumulola Iye—kumulola Iye kuti akudalitseni inu ndi kukupatsani inu vinyo, mkate, Moyo Wamuyaya. Ndiye inu muziwona zinthu mosiyana. Ndiye inu mudza. . . Izo zizikhala mosiyana. Inu simumafuna anyamata kuti azipanga—likhweru la mmbulu kwa inu, likhweru la

nkhandwe, kapena chirichonse chomwe inu mukufuna kulitcha ilo. Ndithudi ayi. Inu mukhala muli wosiyana.

<sup>156</sup> Ndipo inu mukutanthauza kuti mundiuze ine kuti inu mumavala monga chomwecho, ndi kumapita kunja uko, pofuna cholinga china chirichonse? Inu mukuti, “Bwanji, izo zimazizirirapo.” Inu mukuti nathano. Siziri zozizirirapo. Sayansi imatsimikizira kuti izo sizimazizirirapo. N... Ndi kukhumbira komwe kwabwera pa iwe, mlongo. Iwe sukuzindikira izo. Ine sindikuyesera kuti ndikupweteke iwe, koma ine ndikuyesera kuti ndikuchenjeze iwe. Akazi ambiri opanda makhalidwe, wawukhondo basi momwe iye angakhalire, dona wabwino wamng’ono, amayenda ndi zinthu zimenezo, pa msewu, wopanda chikumbumtima cha kudziwa chomwe iye akuchita, chifukwa mlaliki wina wobwerera mmbuyo akuchita mantha kuti amuna anu samapereka zachikhumi mu mpingo aponso. Ngati iye akanakhala atakomana naye konse Melkizedeki, iye sakanati aziganiza zinthu zimenezo. Iye akanati azilalikira Uthenga. Ngati iwo uziwawula chikopa nkuchichotsa pa nsana wake, iye akanati aziulalikira Iwo, mulimonse. Ndizo ndendende kulondola.

<sup>157</sup> Inu mumachita izo, ndipo inu mumachita izo chifukwa kuti mzimu wa kukhumbira wakwera. Ndipo inu amuna omwe mumawalola akazi anu kumachita zinthu za mtundu umenewo, ine ndiri ndi chiyembekezo chochepe pa inu ngati mwamuna. Ndiko kulondola. Ndiko kulondola. Tsopano, palibe chiyamikiro pa izo, chifukwa... kapena palibe kupepesa. Chifukwa, izo nzoona. Mwamuna aliyense yemwe angamulole mkazi wake kupita pa msewu ndi kumakachita monga chomwecho, m’bale, inu mukuyenera kumavala zovala *zake*. Ndiko kulondola. Inu, bwanji, mai!

<sup>158</sup> Ine sindikunena kuti mkazi wanga sangazichite izo. Koma ine ndiyenera kuti ndikhale nditasinthidwa ndi kupotozedwa, ku chimene ine ndiri pakali pano, ngati ine ndingamakhale konse ndi iye pamene iye akuchita izo. Ndipo izo ndi ndendende kulondola.

Asungwana anga, iwo akhoza kuzichita izo pamene iwo ati adzafike pokhala azimayi. Ine sindikuti iwo sangatero. Ine sindikudziwa. Izo ziri kwa chifundo cha Mulungu. Ine ndikuyembekeza iwo sadzatero. Ngati iwo adzatero, iwo azidzapondereza pamwamba pa mapemphero a bambo wolungama. Iwo azidzapondereza pamwamba pa moyo wa winawake yemwe ankayesera kukhala moyo moyenera, ngati iwo ati adzachte konse izo. Ndiko kulondola. Koma ine ndikufuna kumakhala moyo moyenera, kuphunzitsa zoyenera, kukhala moyenera, ndi kumakhoza kuwalangiza iwo moyenera. Ngati iwo ati achite izo, iwo adzapuntha njira yawo waku gehena, pamwamba pa kulalikira kwanga, ndi pamwamba pa Khristu

wanga, ndi pamwamba pa kuchenjeza kwanga, ndiko kulondola, ngati iwo ati adzachite konse izo. Ndithudi. Ndiko kulondola.

<sup>159</sup> Manyazi pa inu. Ngati inu mudzakomane naye konse Khristu, maso ndi maso, ndipo Iye nakudalitsani inu, ndi kuika kupsyopsyona kokuvomerezani uko pa mtima wanu, adierekezi onse mu gehena sadzakupangitsani konse inu kuti muzizivala zimenezo kachiwiri. Ndiko kulondola. Inu mwasintha kuchokera ku imfa kupita ku Moyo, ndipo zokonda zanu zaikidwa pa zinthu zakumwamba ndi osati pa zinthu za padziko lapansi. Ameni. Ine kulibwino ndilisiye phunziro limenelo. Ilo likugirigishya. Chabwino. Koma ndi Choonadi.

<sup>160</sup> Chabwino, pamene ife tikupitirira nazo tsopano mopitirira pang'ono pokha, ndiye ife tikutseka.

*. . . indetu iwo omwe ali ana a Levi, . . . amalandira chachikhumi cha ufindo wa unsembe, ndipo ali nalo lamulo lakuti azitenga chachikhumi cha anthu molingana ndi lamulo, izo ndizo, za abale awo, angakhale iwo adatuluka mchiuno cha Abrahamu:*

*Koma iye amene fuko lake siliri kuwerengedwera kuchokeras kwa iwo omwe analandira zachikhumi za Abrahamu, ndipo anadalitsidwa ndi iye amene anali nalo lonjezo.*

*Ndipo popanda kutsutsana konse wamng'ono amadalitsidwa ndi wamkulupo.*

*Ndipo kuno anthu omwe amafa amalandira zachikhumi; koma apa iye analandira izo, za yemwe ziri kuchitiridwa umboni kuti iye alimoyo. Ndipo ine . . .*

*Ndipo monga ine ndingati . . . ndinene, Levi nayenso, . . . analandira chachikhumi, ankalandira chachikhumi, adapereka zachikhumi mwa Abrahamu.*

*Pakuti iye anali akadali mchiuno cha atate wake, pamene Melkizedeki anakomana naye iye.*

<sup>161</sup> M—matengedwe anu pa za Khristu adzapanga kukhudza kwakukulu pa zomwe ana anu ati adzakhale. Moyo wanu umene inu mukukhala pamaso pa banja lanu uzipanga kukhudza pa chomwe ana anu ati adzakhale. Chifukwa, Baibulo linanena, kuti, “Iye akanati adzachezere kusaeruzika kwa makolo pa ana mpaka ku mibawo yachitatu ndi yachinai.”

<sup>162</sup> Tsopano, mphindi pang'ono zokha, tisanati titseke.

*Ndipo chotero ngati ungwiro (ndi umenewo ungwiro wanu kachiwiri) unali mwa unsembe wa Ulevi, (pakuti pansu pa iwo anthu analandira chilamulo,) pali kusowa kowonjezera kotani kuti abwere . . . wansembe wina awukepo mwa dongosolo la Melkizedeki, ndipo osati ali woitanidwa mwa dongosolo la Aroni?*

<sup>163</sup> Lamulo, amwalamulo, mukuona, “O, inu muyenera kumachita *izi*. Ngati inu simumachita *izi*, sindinu Mkhristu. Ngati inu simumasunga sabata! Ngati inu simu... Ngati inu muzidya nyama! Ngati inu muzichita zinthu *izi*!” Malingaliro onse amwalamulo awa. “Ndipo inu muyenera kuti muzipita ku mpingo. Ngati inu simutero, inu muzilipira chilango pa izo. Inu muyenera kuti muzichita kudzitunduza.” Zinthu izo ndi zachabechabe. Inu mumapulumsidwa mwa chisomo cha Mulungu, mwa kudziwiratu kwa Mulungu, mwa kukonzeratu Kwake. Mulungu anamuitana Abrahamu mwa kukonzeratu, mwa kudziwiratu. Iye anamuitana. Iye anamuda Esau, ndipo anamukonda Yakobo, mmodzi aliyenseyo asanabadwe. Ndiko kulondola. N—ndi kudziwiratu kwa Mulungu komwe kumazidziwa zinthu *izi*.

<sup>164</sup> Inu mukuti ndiye, “Ndi kwa ntchito yanji kulalikira Uthenga?”

<sup>165</sup> Tsopano ine nditi kwa inu, ichi. Paulo anayankha izo, kapena Yesu anatero, kani. Apa ndi Yesu. Iye anati, “Ufumu wa Kumwamba uli monga munthu yemwe anapita ku, d—dziwe kapena kunyanja, ndipo anaponyera umo kombe. Iye anankoka uyo. Kuchokera umo, iye anali ndi akamba. Iye anali ndi nkhasi. Iye anali ndi maserpenti. Iye anali ndi abuluzi. Iye anali ndi achule. Iye anali ndi akangaude. Iye anali ndi amkankhaziwisi. Iye anali—anapezamo nsomba.” Tsopano, bamboyo ankangosodza.

<sup>166</sup> Izo ziri ngati Uthenga. Apa izo ziri tsopano, ine ndikulalikira Uthenga. Ine ndimangoonyera ukonde uko. Ine ndimakoka iwo, ine ndimati, “Onse omwe akufuna, aliyense, muloleni iye abwere.” Apa pamabwera ena, paguwa. Iwo onse amakanirira pa guwa. Iwo amapemphera. Iwo amalira. Ine sindimamudziwa mmodzi kwa mazake. Iyo si ntchito yanga. Ine sindinatimidwe kuti ndidzaweruze.

<sup>167</sup> Koma, alipo ena mmenemo omwe ali achule. Alipo ena omwe ali abuluzi. Alipo ena omwe ali njoka. Ndi, ena, ali kamba. Ndipo alipo ena omwe ali nsomba. Iyo si ntchito yanga kuti ndiweruze. Ine ndikuti, “Atate, ndi *izi* zomwe ine ndatulutsa pokoka.”

<sup>168</sup> Koma, chule anali chule, pa kuyamba pomwe.

<sup>169</sup> Kangaude, kangaude wokalamba akhoza kukhala pamenepo ndi kumayang’ana pozungulira, kanthawi pang’ono, nkuphidigula maso aakulu awo, nkuyang’ana pozungulira, kuti, “Inu mukudziwa chiani? Ine ndangokwanidwa nazo mochuluka Izi momwe ine ndikanapiririra nazo.” Phofu, phofu, phofu, phofu, kutuluka iwo nkumapita.

<sup>170</sup> Dona wokalamba serpenti angadzutse mutu wake mmwamba, ndi kuti, “Chabwino, inu mukudziwa chiani? Ngati iwo azilalikira monga chomwecho, kutsutsana ndi kuvala zazifupi ndi zinthu, izo zimanditengamo ine. Chotero ine

ndichokako ku gulu ilo la oyera-odzigudubuza. Ndizo zonse zomwe zimayenera kuti zinali.” Iwe unali njoka pa kuyamba pomwe. Ndizo ndendende kulondola. Eya.

<sup>171</sup> Ndipo apa pali bambo achikulire a namchidwe, ali ndi chindudu chachikulu icho pakamwa pawo, monga ng’ombe yaku Texas yopanda nyanga, atayima pamenepo ndi kuyang’ana pozungulira, ndi kuti, “Chabwino, izi sizimanditsutsa ine pa kusuta. Ine ndingochokamo mu chinthu ichi, pakali pano.” Chabwino, iwe chule wokalamba, iwe unali chimenecho, pa kuyamba pomwe. Ndiko kulondola ndendende. Ndiko kulondola ndendende.

<sup>172</sup> Chikhalidwe chanu chimatsimikizira zomwe inu muli. Moyo wanu umasonyeza, umanyezimiritsa chomwe inu muli, ndi pachiyambi. Si zovuta kuti ine ndiziwone izo. Si zovuta kuti inu muziwone izo.

<sup>173</sup> Ngati ine nditapita kwa Roy Slaughter mlimi ali apayu, ndipo ine ndikanawona nkhumba ziri pa mulu wa manyowa, zikudya manyowa, ine sindikanaganiza kanthu kena koipa pa izo. Iyo ndi nkhumba. Koma ngati ine ndikanaiwona nkhoa ili apa pa mulu wa manyowa uwo, ine ndikanadabwa. U-nhu. Mukuona? Musati mudandaule, inu simudzamuwona iye pamenepo. Iye sangakhoze basi kupirira nazo izo. Ndiko kulondola.

<sup>174</sup> Ndipo munthu yemwe ali wobadwa mwa Mzimu wa Mulungu amadana nazo zinthu za mdziko. Ndiko kulondola, “Pakuti ngati inu mumakonda dziko kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa inu.”

<sup>175</sup> Ngati ine ndikuyendayenda ndi akazi tsiku lililonse, ndi kubwera umo, kudzamuza mkazi wanga kuti ndimamukonda iye, iye angadziwe kuti ndine wabodza. Zochita zanga zimayankhula momveka kuposa mawu anga. Ndithudi. Ine ndikutsimikizira kwa iye kuti ine sindimamukonda iye, chifukwa ine sindinali woona kwa iye.

<sup>176</sup> Iye akanandiuza ine kuti iye amandikonda ine, ndipo nthawi iliyonse yomwe ine ndikanakhala nditachokapo, iye akanamatengana ndi munthu winawakenso, izo zikanatsimikizira kuti iye sanali kundikonda ine. Kulondola. Zochita zake zikutsimikizira izo. Ine sindikusamala kuchuluka kwake momwe iye akanayesera kuti azindiuza ine, “Bill, ine ndimakukonda iwe, ndipo palibe wina wakenso mu dziko kupatula iwe,” ine ndikanadziwa kuti iye anali wabodza.

<sup>177</sup> Ndipo pamene inu mumayesera kunena kuti, “Ambuye, ine ndimakukondani Inu,” ndi kumachita zinthu za mdziko, Mulungu amadziwa kuti iwe ndi wabodza, pa kuyamba pomwe. Chotero bwanji? Ncha ntchito yanji kulandira chokuchitikira cha mwatheka, ndi chinthu china chonga icho, pamene mlengalenga mwamukulu mwa Kumwamba mwadzaza ndi

chinthu chenicheni? Nchifukwa chiani inu mukufuna kuti mukhale womvetsa chisoni, wodzinenera, wamwatheka, wophikidwa mwatheka, wotchedwa Mkhristu choncho? Pamene, iwe ukhoza kukhala mwana wa Mulungu wobadwa katsopano kwenikweni, uli ndi mabelu achimwemwe akulira mu mtima mwako, ukusangalala, ndi kumamutamanda Mulungu, ndi kumakhala moyo wa chigonjetso kudzera mwa Yesu Khristu.

<sup>178</sup> Osati kumayesera kuzichita izo iwemwini, chifukwa iwe ulephera, pakuyamba pomwe. Koma kumutenga Iye, Awo ndi Mawu Ake, ndi kumapuma pa zomwe Iye anati chinali Choonadi. Ndi kumamukhulupirira Iye, ndi kumamukonda Iye, ndipo Iye azipangitsa chirichonse kugwira ntchito molondola kwa inu. Ndi zimenezo. Ndilo lingalirolo.

<sup>179</sup> Ambuye akudalitseni inu. Sindikufuna kuti ndikuzazireni inu, koma, m'bale, ndi kwabwino kuzaziridwa pang'ono. Ndinu aang'ono anga. Mukuona? Ndipo bambo aliyense yemwe amawakonda ana ake amawakonza iwo ndithudi, kapena iye si mtundu woyenera wa bambo. Nkulondola uko? Ndiko kulondola. Ndipo bambo uyu ali ndi langizo limodzi, ndipo ilo ndi langizo la pakhomo. Ndipo Mulungu ali ndi langizo limodzi lokha, ndipo ilo ndi Mawu Ake.

<sup>180</sup> Ngati ife tikuwakhulupirira Mawu ake, ndiye ife tizikhala moyo mwa Mawu Ake. Ndi ntchito yathu, ngati ife tinayamba takomana naye Mulungu. Osati chifukwa kuti inu mumati, “Chabwino, ine ndimapita ku tchalitchi, ndipo ine ndikuyenera kuti ndizichita *izi*.” Ndiwe womvetsachisoni. Usamachite zimenezo. Chifukwa chiani iwe ukufuna kuti ukhale khwangwala womvetsachisoni, wachinyengo, wopanda umulungu, pamene iwe ukanakhoza kukhala nkunda? Ndithudi. Iwe ukungoyenera kuti chikhalidwe chako chisinthidwe. Ndipo iwe usinthe chikhalidwe chako, ukhale mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu, khala pa mtendere ndi Mulungu.

<sup>181</sup> Yesu! “Chotero Yesu nayenso, kuti Iye akhoze kuwayeretsa anthu ndi Magazi Ake Omwe, anavutika kunja kwa zipata,” Ahebri 13:12 ndi 13. Aroma 5:1, “Chotero pokhala olungamitsidwa mwa chikhulupiriro,” osati mwa kugwirana manja, osati mwa ubatizo wa madzi, osati mwa kusanjikana manja, osati mwa kufuula, osati mwa kuyankhula mu malirime, osati mwa kutengeka kulikonse. “Koma pokhala titalungamitsidwa mwa chikhulupiriro, ife tiri nawo mtendere ndi Mulungu kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.” Ife tadutsa kuchokera ku imfa tapita ku Moyo, ndipo takhala zolengedwa zatsopano, chifukwa ife takhulupirira pa Mwana wobalidwa yekha wa Mulungu, ndipo tamulandira Iye ngati Mpulumutsi wathu wathu. Ndipo Magazi Ake akuchita, usikuuno, ngati chitetezero cha tchimo lathu, kuti aziima mu malo athu.

182 Mu Chipangano Chakale, muli malo amodzi okha oti ukhale nacho chiyanjano, ndiwo pansi pa magari. Wokhulupirira aliyense ankayenera kuti abwere pansi pa magari. Pamene ng'ombe yofiira inali kuphedwa, iyo inali kupangidwira kwa nsembe ya tchimo. Iyo inkayenera kukhala ili yofiira. Ndipo mutu wa 19 wa Eksodo, ngati wina aliyense wa inu akanafuna kuti awerenge izo. Ndipo iyo inkayenera kuti itengedwe, zopondera, zonse, ziwotchedwe palimodzi. Ndipo izo zinali kupangidwa kukhala madzi olekanitsa. Izo zinali kukaikidwa kunja kwa zipata. Izo zimayenera kuti zigwiridwe ndi manja oyera. Magazi a ng'ombe iyi ankapita patsogolo...kwa osonkhana, ndipo ankapakidwa kasanu ndi kawiri pa khomo. Ndipo tsopano, munthu wodetsedwa aliyense akamayenda nadza, ankayenera poyamba kuzindikira ndi kuwawona magari awo, ndi kuzindikira kuti pali chiyanjano pansi pa magari amenewo pokha. Ndiwo malo okha omwe wopembedza akanati makamaka apembedze mololezedwa, panali pansi pa magari.

183 Ndiye, chinthu choyamba chimene iye ankayenera kuti achite, iye asanabwere pansi pa magari, pankayenera kuti pakhale madzi a kulekanitsa awa atakonkhedwa pa iye, ndipo wosayeretsedwayo ankapangidwa kukhala woyera.

184 Ndipo iwo ankatenga madzi olekanitsa ndipo ankawakonkha iwo pa munthu wolowererayo, ndipo iwo ankamulekanitsa iye kwa tchimo lake. Ndiyeno iye ankayenda pansi pa milozo isanu ndi iwiri ya magari iyi, ndipo ankakhala ndi chiyanjano ndi okhulupirira ena onsewo mu Kukhalapo kwa Mulungu.

185 Pali njira imodzi yokha yochitira izo. Osati kugwirana chanza, osati kujowina mpingo, osati mwa maubatizo, osati mwa zotengeka; koma kuyenda mpaka ku madzi a kulekanitsa, kusanjika manja ako, mwa chikhulupiriro, pa mutu wa Yesu, ndi kuti, “Ndine wochimwa, ndipo Inu munafa mmalo mwanga. Ndipo Chinachake mkati mwa ine chikundiiza ine kuti Inu mundikhululukira ine machimo anga, ndipo ine ndikukulandirani Inu ngati Mpulumutsi wanga wanga tsopano.” Nkuyenda pansi pa Magazi, kutaliko, nkumakhala ndi chiyanjano ndi ana a Mulungu. Ndi zimenezo. Nkumadya mkate, kumamwa vinyo, ndi kumakhala nacho chiyanjano ndi mpingo.

186 O, kodi Iye si wodabwitsa? Kodi Iye si wabwino? Tsopano, izi zikhocha kuwoneka zachilendo kwa iwe, mzanga. Koma chiani—ndikuimira chiani pano ndi kumanena zinthu izi? Kodi ine ndingamanene izo poyesera kudzipanga ndekha wosiyana kwa munthu wina aliyense? Ngati ine nditero, ndiye ine ndikusowa kuti ndilape. Ine ndikunena Izi chifukwa Mulungu anazinena Izo, chifukwa Iwo ndi Mawu a Mulungu. Ndipo mvetserani. Pali kubwera nthawi, ndipo tsopano ilipo, yomwe kuti anthu azidzapita kuchokera kummawa mpaka kumadzulo, kuyesera kuti apeze Mawu a Mulungu, ndipo osakhoza kuwapeza Iwo.

<sup>187</sup> Pamene inu mupita mu msonkhano, chinthu choyamba chomwe inu mumachita, inu mumapita mmenemo ndi kukakhala ndi mulu wa malirime ndi kutanthauzira, ndipo winawake amaimirira ndi kukhala akubwereza Malemba; ndipo izo nzachithupithupi. Mwamtheradi. Mulungu ananena kuti ife “tisamagwiritse ntchito kubwereza kwachabe,” nanga bwanji Iyeyo? Ngati Iye anzilemba Izo kamodzi, inu muzikhulupirira Izo. Iye samasowa kuti azinenenso Izo kachiwiri. Malirime ndi kutanthauzira ndi zabwino, koma izo zizikhala uthenga wolunjika kwa mpingo ndi kwa winawake, osati basi zachithupithupi ndi zinthu monga izo. Ndiyeno inu mumapita patsogolo mu zinthu zina zonse izi.

<sup>188</sup> Kuno tsiku lina, amuna awiri anayenda nalowa...ndipo mwamuna ndi mkazake, ndi mwamuna wina ndi mkazake, aang'ono atangokwatirana kumene, anayenda nalowa mu malowo, kuti azipita ku Afrika ngati amishonare. Winawake anaaimirira ndipo anapereka ulosi, ndipo anapereka malirime ndi kutanthauzira, kuti, “Iwo anatengerana mkazi wa wina ndi mzache.” Kutu, “Izo sziyenera kuti zikhale mwa njira imeneyo. Iwo anakwatira munthu wolakwika.” Ndipo anthu awiri awo analekana ndipo anakwatiranso, kachiwiri. Mwamuna wina anatenga mkazi wa winayo, mmodzi winayo, mu chipembedzo chotsogola cha Chipentekoste, ndipo anapita ku Afrika ngati amishonare.

<sup>189</sup> M'bale, pamene iwe utenga lumbiroo lako, umakhala wokakamizidwira ku lumbiroo limenelo mpaka imfa itakumasula iwe. Kulondola ndendende. Ndithudi. Pamene iwe utenga lumbiroo lako, ilo ndi lomangiriza.

<sup>190</sup> Zachabechabe, zonsezo! Ndipo izo zafika pa malo pamene iwe upita ku mipingo, mwina iwo ndi ozizira kwambiri ndi ofunda ndi owuma, mpaka choyezera uzimu chimapita fifite pansu pa ziro. Anthu amangokhala ngati mavu pa achali, owawasa basi ndi osayanjanitsika ndi owuma. Ndipo ngati iwe umumva winawake, kutali kumbuyo uko mu ngodya, akhoza kunena pang'ono mwamanzenene “ameni,” kamodzi mu kanthawi, kukhala ngati zikuwapweteka iwo, onse a iwo amaongola makosi awo ngati atsekwe, kuti ayang'ane mozungulira, awone chomwe chinachitika. Inu mukudziwa icho ndi choonadi. Ine sindikunena izo mwa nthabwala. Ano si malo ochitirapo nthabwala. Izo ndi Choonadi. Kulondola. Ine ndikunena izi chifukwa ndi Choonadi cha Uthenga.

<sup>191</sup> Ndipo kumbali inayo, inu mumapeza gulu la zachabechabe za gulu la otengeka mwachithupithupi akupitiriza nazo, ndipo Mawu owona a Mulungu potsiriza afika pa malo pomwe iwe sungakhoze kuwamva Iwo mpang'ono pomwe: pakati pakale pa msewu, Uthenga, Kuwala kwa pa njira yanga, aleluya, Magazi a Mwanawankhosa, chikondi cha Mulungu chomwe chimatilekanitsa ife kwa zinthu za mdziko.



192 “Kodi inu munayamba mwayankhulapo mmalirime, m’bale? Inu mulibe Iwo. Kodi inu munafuula mpaka kumverera kuzizira kukuyenderera pa nsana wanu? Kodi inu munawona mipira ya moto?” O, zachabechabe! Palibe chinthu choterocho.

193 Kodi inu mwakhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu ndi kumulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu wanu? Ndipo Mzimu wa Mulungu ukumachitira umboni limodzi ndi mzimu wanu, kuti ndinu mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu. Ndipo moyo wanu ukubala chipatso cha chikondi, chimwemwe, mtendere, kupirira, ndi kufatsa, ubwino. Ndiye ndinu Mkhristu. Ngati iwo sukutero, ine sindikusamala zomwe inu mukuchita.

Paulo anati, “Ine ndikhoza kupereka thupi langa kuti aliwotche ngati nsembe. Ine ndikudziwa zinsinsi zonse za Mulungu. Ine ndikhoza kusuntha mapiri ndi chikhulupiriro changa. Ine ndikhoza kuyankhula mmalirime onga a anthu ndi a Angelo. Ine sindiri kanthu.” Nanga bwanji zimenezo? Akorinto Woyamba 13; kafufuzeni ngati Izo ziri zolondola kapena ayi.

194 Tsopano kafufuzeni ng—ngati Akorinto, Akorinto Wachiwiri 13, ine ndikukhulupirira ndi pomwe pali. Kapena, chabwino, mwina ndi Akorinto Woyamba kapena Wachiwiri. Pa Akorinto Woyamba apo, Akorinto Woyamba 13, ndi kulondola. “Ngakhale ine ndingayankhule ndi malirime a anthu ndi a Angelo, limodzi mtundu womwe ungakhoze kutanthauziridwa ndi omwe sangakhoze kutanthauziridwa, ine sindiri kanthu.” Chotero ncha ntchito yanji kumapusidwa ndi izo, ndiye?

195 “Ngakhale ine ndingamvetse zinsinsi zonse za Mulungu.” Chifukwa chiani inu mumapita ku maseminare ndi kukayesera kuti mukaphunzire zochuluka kwambiri za izo? Inu kulibwino mukhale mwabwino ndi Mulungu, poyamba. Ndithudi. “Ngakhale ine, ‘O, adalitsidwe aleluya!’”

196 Inu mwafika poti inu simungathe ngakhale kukhala ndi osonkhana kupatula ngati inu mukhale ndi kukopa kwa machiritso kapena mtundu wina wa zozizwitsa zikuchitikapo. “M’badwo wofooka ndi wachigololo umafunafuna zoterozo.” Inu mukuzifunirani izo?

197 Paulo anati iye akanakhoza kumachita mitundu yonse ya zinthu, ngakhale kusuntha mapiri, ndipo apobe iye si kanthu. “Pamene kuli malirime, iwo adzaleka. Pamene kuli chidziwitso, icho chidzachoka. Pamene kuli mauneneri, iwo adzalepheraka. Koma pamene icho chimene chiri changwirowo chidzabwera, icho chidzakhalapobe kwanthawizonse,” ndipo chikondi ndicho ungwiro. “Mulungu analikonda kwambiri dziko, kuti Iye anapereka Mwana Wake wobalidwa yekhayo.” Kuti, “Aliyense amene anjenjemera, aliyense amene agwedeza, aliyense amene ayankhula, yense?” “Aliyense yemwe akhulupirira mwa Iye asadzawonongeke, koma kukhala nawo Moyo Wamuyaya.” Khulupirirani izo, ananu.

198 Iwo amayesera kuzipangitsa izo kukhala zovuta kwambiri, zinthu *izi* ndi zinthu *izo*. Pamene, izo zimabwatamira mpaka ku chinthu chimodzi chomwecho: chikhulupiriro chanu chomwe mwa Mulungu. Ndicho icho. Izo zimanena icho. “Pakuti mwa chikhulupiriro,” osati mwa kumverera. “Mwa chikhulupiriro,” osati mwa zotengeka. “Koma mwa chikhulupiriro inu mumapulumsidwa; ndipo izo mwa...” Chifukwa inu munawafunafuna Ambuye? Chifukwa inu munali munthu wabwino? Chifukwa, “Mulungu, mwa chisomo, anakudziwiranitu inu ndipo anakudzozereranitu inu ku Moyo Wamuyaya.”

199 Yesu anati, “Palibe munthu angathe kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye. Ndipo onse omwe adza kwa ine, Ine ndidzamupatsa iye Moyo Wamuyaya. Palibe munthu angawakhwatule iwo kuchokera mdzanja Langa. Iwo ndi Anga. Iwo anapulumsidwa kwanthawizonse. Ine ndawatenga iwo. Palibe munthu yemwe angawakhwatule iwo kuchokera mdzanja la Atate Anga, ndipo Iye ndi Yemwe anawapereka iwo kwa Ine. Iwo ndi mphatso zachikondi Zanga.”

200 “Ndipo onse omwe Iye anawadziwiratu, Iye anawaitana.” Iye samamuitana aliyense kupatula Iye atamudziwiratu iye. “Onse amene Iye anawaitana, Iye anawalungamitsa; onse omwe Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsa ulemerero.” Chotero, inu mukuona, ife tiri pa mpumulo wangwiro basi.

201 Tsopano, ine ndikudziwa pali amwalamulo ambiri pano, nainte naini pa zana a inu. Koma, onani, ngati inu mutangoti mutenge Izi ndi kuzindikira kuti ine sindikuyesera kuti ndinene kwa inu chinachake.

202 Ndiye inu mukuti, “Chabwino, M’bale Branham, ine nthawizonse ndakhala ndikulingalira kuti ndimayenera kuti ndichite *izi* ndi kuyenera kuchita *izo*.” Pali kusiyana kot—kotero mmenemo, m’bale, zomwe iwe uyenera kuti uzichite ndi zomwe iwe ukufuna kuti uzichita. Iwe umapulumsidwa, osati chifukwa iwe unali ndi chinthu chimodzi chochita ndi icho. Iwe umapulumsidwa chifukwa kuti Mulungu anakupulumutsa iwe asanaikidwe maziko a dziko.

203 Mvetserani. Mvetserani apa. Baibulo linanena, mu Chivumbulutso. Ine ndikutengerani inu kuchokera koyamba mpaka kotsirizira tsopano. Baibulo linanena, mu Chivumbulutso, kuti, pamene chirombo chinabwera, iye anawanyenga onse a pa dziko lapansi. Chirombo chinatero. “Iye anawanyenga onse okhala pa dziko lapansi, omwe maina awo sanali atalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa...” Kuchokera pamene chitsitsimutso chinayamba? Kodi izo zikumveka molondola? Chabwino, kuchokera pamene mlaliki analalikira ulaliki wamphamvu

uja? Kuyambira pomwe munthu ujayu anachiritsidwa? “. . . kuchokera ku maziko a dziko.”

<sup>204</sup> Kodi Yesu anaphedwera kuti, pa Kalvare? Ayi, bwana. Yesu anaphedwa asanaikidwe maziko a dziko. “Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu, yemwe anaphedwa asanaikidwe maziko a dziko.” Mulungu, pachiyambi, pamene Iye analiwona tchimo, Iye anawona zomwe zikanati zidzachitike, Iye anayankhula Mawu. Ndipo Yesu anaphedwa asanaikidwe maziko a dziko. Ndipo munthu aliyense yemwe anapulumutsidwa, anapulumutsidwa, malingana ndi Baibulo, pamene Mwanawankhosa anaphedwa mu malingaliro a Mulungu, asanaikidwe maziko a dziko. Inu munaphatikizidwira mu chipulumutsocho pamenepo. Chotero kodi inu muchita nazo chiani Izo?

<sup>205</sup> Ndi Mulungu. Lodala likhale Dzina la Ambuye! “Ndi Mulungu yemwe akugwira ntchitoyo; si iye yemwe afuna kapena iye yemwe athamanga, koma Mulungu yemwe akusonyeza chifundo.”

Ngati Yesu anaphedwa asanaikidwe maziko a dziko, izo zinatenga zaka zikwi zinai izo zisanachitike kwenikweni. Koma pamene Mulungu anayankhula izo kumbuyo kuno, Mawu aliwonse a Mulungu ndi okhazikika. Iwo ndi osatontholetsedwa. Iwo ndi osagawanika. Iwo sangathe kulephera. Ndipo pamene Mulungu anamupha Mwana asanaikidwe maziko a dziko, Iye anali ataphedwa mochuluka pamenepo monga Iye analiri pa Kalvare. Icho ndi chinthu chotsirizidwa, pamene Mulungu anena chomwecho. Ndipo kumbukirani, pamene Mwanawankhosa anaphedwa, chipulumutso chanu chinaphatikizidwira mu nsembeyo, chifukwa Baibulo limanena kuti dzina lanu “Linalembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa asanaikidwe maziko a dziko.”

Nanga bwanji zimenezo? Ndiye kodi ife tichitapo chiani? Ndi Mulungu yemwe amasonyeza chifundo. Ndi Mulungu yemwe anakuitanani inu. Ndi Mulungu yemwe anakusankhani inu mwa Khristu asanaikidwe maziko a dziko. Yesu anati, “Inu si—inu simunandisankhe konse ine. Ine ndinakusankhani inu. Ndipo Ine ndinakudziwani inu, asanaikidwe maziko a dziko.” Ndi inu apo.

<sup>206</sup> Chotero, mukuona, izo zimachotsa mantha kwa inu. “O, ine ndikudabwa ngati ine nditi ndipitirire kugwiritsabe? Ine ndikwanitsa izo, Mulungu adalitsidwe, ngati ine nditi ndipitirire kugwiritsabe.” Izo si kuti ngati ine ndigwiritsabe, kapena ayi. Izo ndi ngati Iye anagwiritsa, kapena ayi. Ndi z—zomwe Iye anachita, osati zomwe ine ndinachita. Ndi zomwe Iye anazichita.

Kodi izo ziri pansu pa lamulo lachiwombolo? Ichi ndi chinthu chaching’ono chomwe ine ndikufuna kuti ndichinene ndisanati nditseke.

<sup>207</sup> Nanga bwanji ngati kavalo wamkulu akanabala bulu wamng'ono? Ndipo bulu wamng'ono uyo akanakhala ndi makutu ake onse othyokera pansi. Iye nkukhala wa maso-opingisana, ndi mawondo-oguluka, miyendo-yamatewe. Mchira wake woloza molunjika mmwamba mu mlengalenga. Chinyama chake chowoneka moyipacho! Bwanji, aliyense. . . Ngati bulu wamng'ono uyo akanati aganize, kuti, "Tsopano, dikirani miniti. Pamene iwo azituluka kuchokera mnyumbamo mmawa uno, ine ndikukuuzani inu, ine ndithudi andikhoma pamutu. Chifukwa, iwo sandidyetsa ine konse. Taonani chinthu chowoneka-moipa chomwe ine ndiri. Ine ndiribe ngakhale konse mwayi."

<sup>208</sup> Chabwino, uko nkulondola. Inu mulibe konse mwayi. "Chabwino, ine ndinabadwa mu dziko lino, koma taonani apa chinthu chowoneka-moipa chomwe ine ndiri. Chotero i—i—i. . . ine sindikhala nawo konse mwayi. Ine sindikwanitsa izo. Ine sindingathe kuzikwanitsa izo." Mukuona?

<sup>209</sup> Koma nanga bwanji ngati mayi wake ali wolangizidwa kwenikweni mu lamulo? Iye akanati, "Mwananga, iko nkulondola. Ndiwe yense wosawumbidwa mwabwino, ndipo sindiwe woyenera nkomwe kuti uzidya chakudya cha padziko lapansi. Ndiko kulondola. Sindiwe woyenera. Koma, mwananga, mwanjira ina imzake, iwe ndi woyamba wanga. Ndipo, iwe ukudziwa, iwe unabadwa pansi pa ufulu wobadwa nao. Ndipo wansembe sadzakuwona konse iwe. Koma, kwa dzina lako, payenera kuti pakhale pali mwanawankhosa wosalakwa wopanda chilema, ayenera kuti afe mmalo mwako, chotero kuti iwe ukhoze kukhala moyo."

<sup>210</sup> Chabwino, bulu wamng'ono uyo akanakhoza kumenyetsa zitendene zake mmwamba ndi kukhala ndi nthawi yaikulu. Sizikupanga kusiyana kulikonse chomwe iye ali, chifukwa iye sadzawonedwa konse ndi woweruza, wansembe. Ndi mwanawankhosa yemwe ansembe amayang'anapo. Osati buluyo; mwanawankhosa!

<sup>211</sup> Ndipo ndi Khristu yemwe Mulungu amayang'anapo, osati inuyo. Ndi Khristu. Chotero ngati mulibe cholakwika mwa Iye, pangakhoze bwanji kukhala cholakwika? Iye angakhoze bwanji kupeza cholakwika, pamene inu muli okufa ndipo moyo wanu wabisika mwa Khristu kudzera mwa Mulungu, mutasindikizidwa ndi Mzimu Woyera? "Iwo amene ali obadwa mwa Mulungu samachita tchimo, pakuti iye sangakhoze kuchimwa." Iye angathe bwanji kuchimwa pamene nsembe yangwiro ili apo mmalo ake? Mulungu samayang'ana konse pa ine, Iye amayang'ana pa Khristu, chifukwa ife tiri mwa Khristu.

<sup>212</sup> Tsopano, ngati ine ndikumukonda Khristu, ine ndizikhala moyo ndi Iye. Iye sakanati andibweretse konse ine umo kupatula ngati Iye atadziwa. Ngati Mulungu akanandipulumutsa ine lero, akudziwa kuti Iye akanati anditaye ine mu masabata

asanu ndi limodzi kuchokera lero, Iye akugonjetsa cholinga Chake Chomwe. Kulondola. Iye sakudziwa nkomwe tsogolo ndiye, ngati Iye anandipulumutsa ine, akudziwa. Iye akufuna andipulumutsire ine chiani, akudziwa kuti Iye anditaya ine? Mulungu samachita zinthu, ndiye nkuzilandanso izo mu masabata awiri, kuti asunge lonjezo Lake. Pamene Iye akupulumutsani inu, izo ndi za kwa nthawi ndi Muyaya.

<sup>213</sup> Tsopano, inu mukhoza kutengeka, ndi kuti, “O, inde, Mulungu adalitsidwe! Aleluya! Ine ndinayankhula mu malirime. Ine ndinafuula. Ine ndamupeza iye. Aleluya!” Izo sizikutanthauza kuti inu muli nawo Iwo. Koma, m’bale, pamene chinachake chibwera mmusi *umu*, ndi inu mutazikika naye Khristu, ndiye zipatso za Mzimu zimakutsatirani inu. Ife timachitira umboni, mzimu wathu ndi Mzimu Wake, kuti ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Chonde khalani nacho Icho, amzanga.

<sup>214</sup> Ine ndikusungani inu pano usiku wonse, ndikuyankhula za izo. Ine ndimazikonda Izo. Ine ndikukukondani inu. Ine ndimabwerera ku kachisi wamng’ono uyu, nthawi pambuyo pa nthawi, ngati Mulungu angati awusunge moyo wanga. Ine ndikufuna kukuwonani inu mutazikika ndi kukhazikika mu Chikhulupiriro choyera icho. Ine sindikufuna kumakuwonani inu mukukankhidwira uku ndi uko, ndi mphepo yaing’ono iliyonse ya chiphunzitso ingabwerepo kuno, ndi kukugwedezeni inu, ndi kupitiriza nazo, ndi kukhala ndi magazi pang’ono mmanja mwawo, kapena thukuta pang’ono pa nkhope zawo, kapena chinachake chimzake, ndi kumawona mtundu wina w—w—wa kuwala patsogolo pawo, mtundu wina wa—chinthu chakudzikonda, monga Baibulo linanena, “Kutukumuka mu mtima mwake, ndipo asanawone kanthu.” Ndiko kulondola. Ine ndikufuna inu kuti mukhale olimba pa Mawu. Ngati iwo ali PAKUTI ATERO AMBUYE, zikhalani nawo Iwo, zikhalani nawo moyo Iwo. Iwo ndi Urimu Tumimu wa tsiku lino. Mulungu akufuna kuti inu muzikhala moyo ndi Iwo. Ngati izo siziri mu Mawu, ndiye iwalani za izo. Zikhalirani moyo Mulungu, zikhalirani moyo Khristu.

<sup>215</sup> Ndipo ngati mtima wanu uyamba kusochera pamenepo, inu muzidziwa kuti pali chinachake chomwe chachitika, zibwererani ku guwa ndi kukati, “Khristu, ndibwezeretseni . . . chimwemwe cha chipulumutso changa. Perekani kwa ine chikondi chija chomwe ine ndinali nacho nthawiina. Icho chikutaikamo, Ambuye. Pali chinachake chimene ine ndachichita. Ndipangeni ine kukhala woyera kachiwiri, kuima. O Ambuye, palibe chimene ine ndingakhoze kuchita. Ine sindingathe kusiya *izi* ndi kusiya *izo*. Ine ndikuyang’ana kwa Inu kuti muzichotse izo mwa ine, Ambuye, ndipo ine ndikukukondani inu.”

<sup>216</sup> Ndipo nkuchoka pa guwa ilo, munthu watsopano mwa Khristu Yesu. Ndiye inu simudzasowa kuti muzidalira pa mpingo wanu, kudalira pa wansembe wanu, kudalira pa m'busa wanu. Inu mukudalira pa Magazi okhetsedwa a Ambuye Yesu. "Mwa chisomo inu munapulumsidwa."

Tiyeni ife tipemphere.

<sup>217</sup> Ambuye, kuphunzitsa kolimba choteroko! Ndi nthawi yomwe mpingo waung'ono uno ukuyenera kuti uzidya nyama, ndipo osatinso mkaka wa Mawu. Ife takhala mochuluka kwambiri mu mkaka tsopano, kumupatsa mwana botolo lake. Koma ife tiyenera kuti tizikhala nazo nyama zolimba, pakuti tsikulo liri kuyandikira. Nthawi zazikulu zowopsya ziri pafupi, ndipo mavuto ambiri ali pa njirayi. Ndipo ife tikudziwa kuti sipadzakhala nthawi yabwinoko. Ife tikudziwa kuti tiri pa mapeto. Nthawi zizipitirira kumaipira ipirabe mpaka Yesu atadza, malingana ndi Malemba.

<sup>218</sup> Ife sitingakhoze kuwalonjeza iwo kanthu kalikonse mu moyo uno. Koma mu moyo ukudzawo, ife tikhoza kuwalonjeza iwo Moyo Wamuyaya kudzera mu Mawu Anu, ngati iwo ati akhulupirire pa Mwana wa Mulungu ndi kumuvomereza Iye ngati chitetezero chawo, monga Mmodzi yemwe anaima mu malo awo, ngati Mmodzi yemwe anatenga machimo awo. Perekani izi tsopano.

<sup>219</sup> Mulole osakhulupirira akhale okhulupirira. Mulole odzinenera mpingo, pano usikuuno, omwe adzinenera chipembedzo ndi kumangokhala mu mpingo, mulole iwo alandire chowachitikira ndi Mulungu; kuti chikondi choteroko chibwere mu mtima mwawo, kuti iwo azilira chifukwa cha machimo awo, afe kwa iwoeni, ndi kubadwa mwatsopano mwa Mzimu Woyera, ndi kukhala ofatsa ndi achifundo, achikondi, ndi odzaza chimwenwe ndi madalitsa. Kumakhala moyo wotero, mpaka iwo akhale okolera kwambiri kuti aziwapangitsa anthu omwe ali powazungulira iwo, kuchita ludzu lofuna kuti akhale monga iwo. Perekani izi, Ambuye, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake.

Ndipo ndi mitu yathu yoweramitsidwa.

<sup>220</sup> Ine ndikudabwa, usikuuno, ngati pangakhale mmodzi pano, akuti, "M'bale Branham, ngati ine ndikanayezedwa mu muyezo wa Mulungu pa nthawi iyo, ine sindikanakhoza nkomwe, nkomwe, kukhoza kufikira zoyenerereza zomwe inu mukuzikambazo usikuuno. Ine ndikufuna inu kuti mundikumbukire ine mu pemphero, kuti ine ndisithe njira zanga, ndipo Mulungu abwere mkatimu ndi kuchotsamo zachabechebezi mkati mwanga ndi kundipanga ine Mkristu weniweni"? Kodi inu mungakweze dzanja lanu pofuna pemphero, ng—ngati inu mungatero? Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu,

kumbuyo. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, m'bale wamkulu. Mulungu akudalitseni inu, mlongo.

Woyera, Woyera, Woyera, Ambuye Mulungu  
wamakamu,  
Kumwamba ndi dziko mwadzaza Inu,  
Kumwamba ndi dziko zitamanda Inu,  
Ambuye Wammwambamwamba.

<sup>221</sup> “Woyera.” Pamene inu mukuganizira tsopano, mukupemphera, pamene inu mukumverera kukhutitsidwa kuti mwakhala mukulakwitsa, ndipo inu mukufuna kukhala moyenera, kodi inu mungangokweza dzanja lanu, mukuti, “Mulungu, ndipangeni ine chomwe ine ndikuyenera kuti ndikhale ndiri?” Mulungu akudalitse iwe, dona wamng’ono. “Mulungu, ndipangeni ine chimene ine ndikuyenera kukhala ndiri.” Mulungu akudalitseni inu, m'bale, mlongo, inu, inu, inu cha *apa*.

<sup>222</sup> Tsiku likufa. Ine ndikudziwa kuti ndi zovuta, amzanga, koma ndi bwinoko kudziwa Choonadi tsopano. Tsopano mwakachetechete zipempherani.

Woyera, Woyera, Woyera, Ambuye Mulungu . . .

Iye ndiye woyera, yekha.

. . .ladzaza ndi Inu,  
Kumwamba ndi dziko zitamanda Inu,  
O Ambuye Wammwambamwamba.

<sup>223</sup> Atate Akumwamba, pamene dzuwa limakalowa kumadzulo, mpheta zimasonkhana mmitengo ndi zokonedwa zawo. Mbalame zonse zimapita ku zisa zawo. Nkhunda zimawulukira pa mawaya, mmwamba, kuti njoka zisamazivutitse izo kupyola mu usiku. Izo zimakhala pamenepo ndi kumalira kwa ina ndi imzake mpaka zitafika pogona. Dzuwa potsiriza limalowa.

<sup>224</sup> Tsiku lina ife tikubwera ku ora limenelo. Kulowa kwa dzuwa kudzachitika. Ine sindikudziwa ndi liti, Ambuye. Koma pali anthu pano usikuuno omwe akhutitsidwa kuti iwo akhala akulakwitsa, ndipo iwo akufuna kuti abwere ku malo amenewo . . .Monga Lincoln anabwera kwa iwo pamene iye anali kufa, anati, “Tembenezirani nkhope yanga cha kolowera kwa dzuwa.” Ndipo iye anayamba, “Atate Athu Omwe muli Kumwamba.”

<sup>225</sup> Monga Moody wakale anati, “Kodi iyi ndi imfa? Ili ndi tsiku langa lovekedwa korona.”

<sup>226</sup> O Inu Wamuyaya, alandireni iwo pakali pano; mwa chikhulupiriro, pamene iwo akhala apo mu mipando yawo. Inu munagoda pa mtima wawo, pa mpando wawo. Limenelo ndilo guwa lawo. Ino ndi nthawi yoti Inu muwalandire iwo, pakali

pano. Inu munati, “Iye amene adza kwa Ine, Ine sindidzamutaya mwa njira iliyonse.”

<sup>227</sup> Ndipo tsiku lina pamene dzuwa lizidzalowa, mkazake kapena mwamunake ataima pafupi ndi kama, madotolo atayenda kuchokapo. O Woyera, Woyera, kutonthola kokongola, kokoma uko, basi dzuwa lisanalowe. Pamene ife tingakhoze kuwuka apo ndi kuti:

Kulowa kwa dzuwa ndi Nyenyezi ya Usiku,  
Ndi kuitana kumodzi komveka kwa ine;  
Ndipo mulole pasadzakhale kubuula pa malo  
awo

Pamene ine ndizidzakankhira ku nyanja.

<sup>228</sup> O Mulungu, perekani izi kwa iwo ora lino; pamene iwo akudikira, kudikirira mdalitso wa Mulungu kuti udze pa iwo. Tengani zonse za kupsya mtima, zonse chidziko, zichoke kwa iwo, ndi kulenga mwa iwo mtima watsopano. Inu munati, “Ine ndidzachotsamo mtima wakalewo, ndi kuikamo mtima wa mnofu. Ndipo ine ndidzaika Mzimu Wanga mu mtima umenewo, ndipo iwo azidzayenda mu malangizo Anga ndi kumasunga malamulo Anga.” Chifukwa, ndi langizo la chikondi, ndipo si la ntchito. Ndi la chikondi. Ndipo chikondi chimatikakamiza ife kuti tizichita izo. Ndi ntchito ya chikondi, kuti izitikakamiza ife. Ndi ntchito yathu kuti tizitsatira chikondi. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mupereke izi kwa mtima uliwonse umene unakweza nkono wake usikuuno.

<sup>229</sup> Ndipo awo omwe sanakweze dzanja lawo, mulole iwo tsopano, mwa chisomo, akweze manja awo kuti akulandireni Inu, ndi kuti adzazidwe ndi Mzimu Wanu mwa njira yofatsa, ndi yokoma, yakachetechete, yodzichepetsa iyi; ndi kukhala odzaza chisomo, achoke pano monga munthu wosinthika. Momwe mbalame ziziimbira mosiyana, momwe aliyense ati akhalire wosiyana, likatha ora lino, O Ambuye Wammwambamwamba.

Woyera, Woyera, Woyera, Ambuye Mulungu  
wamakamu,  
Kumwamba ndi dziko mwadzaza Inu,  
Kumwamba ndi dziko zitamanda Inu,  
O Ambuye Wammwambamwamba.

<sup>230</sup> Inu tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa, inu omwe munakweza manja anu kuti mukumbukiridwe mu pemphero, kodi inu mukumverera ngati kuti Mulungu wayankhula kwa inu mwa njira yoteroyo tsopano, osati mwa kutengeka, koma basi chinachake pansu pomwe mkati mwa inu. Inu mukumverera ngati kuti Mulungu wakupatsani inu Moyo Wamuyaya? Inu mukumverera ngati kuti inu muzituluka mu tchalitchi monga munthu wosiyana? Kodi inu mungakweze manja anu kumbuyoko usikuuno? Mulungu akudalitse iwe, mwananga. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Mulungu akudalitseni,



mlongo. Mulungu akudalitseni inu. Ndiko kulondola. “Ine ndizipita kuchokera ku mpingo uno, usikuuno, munthu watsopano.” Makanda obadwa mwatsopano mu Ufumu wa Mulungu.

<sup>231</sup> Chinachitika ndi chiani? Ine ndikudziwa ndi dongosolo la kubwera ku guwa. Ilo ndi guwa Lachimethodisti. . . dongosolo Lachimethodisti, ine ndikutanthauza. Ilo linayambitsidwa mu mpingo wa Chimethodisti, mu masiku a Joni Wesile. Izo sizinalipo konse mu masiku a Baibulo. “Onse omwe ankakhulupirira ankawonjezedwa kwa Mpingo.” Inu mukhoza kukhulupirira paliponse pomwe inu muli, kunja pabwalo, kunja mu msewu, paliponse, paliponse. Paliponse, izo sizimapanga kusiyana kulikonse, choncho basi pamene inu mukumulandira Khristu ngati Mpulumutsi wanu wanu. Ndi kuchita kwa Mzimu Woyera komwe kumabwera mu mtima mwanu. Pamene inu mwamukhulupirira Iye, kumulandira Iye, inu mwadutsa kuchokera ku imfa mwapita ku Moyo, ndipo inu mwakhala zolengedwa zatsopano mwa Khristu Yesu.

Msandipitire, Mpulumutsi,

Tsopano imani pa mapazi anu.

. . . kulira kwanga;

Pamene muchezera ena,

Msandipitire.

<sup>232</sup> Tsopano ine ndikufuna mnyamata ndi dona, omwe ine ndikuzindikira kuti ndi mkazi wake, omwe munakweza dzanja lanu, ine ndikufuna kuti inu mukweze dzanja lanu kachiwiri kumbuyo uko; mwananga, wavala chikhoto chofiira, ndi dona, omwe amuvomereza Khristu ngati Mpulumutsi wao wao. Mnyamata wakhala apayu mu chikuku, wamulandira Khristu ngati Mpulumutsi wake, anamverera kuti Mulungu wamupulumutsa iye. Ndi ena kumbuyo uko omwe munakweza manja anu, akwezeni iwo kachiwiri kuti anthu akhoze kuyang’ana pozungulira, akhale nacho chiyanjano ndi inu.


<sup>233</sup> Agwireni dzanja lawo, winawake pozungulira, mwaima pafupi ndi iwo. Itini, “Mulungu akudalitseni inu. Mwalandiridwa mu ufumu wa Mulungu, m’bale wanga, mlongo wanga.” Chiyanjano, ndi chomwe ife tikuchifuna. Mulungu akudalitseni. . . Gwirani chanza ndi mnyamata uyu apa mu mpando. Ambuye akhale ndi iye. Uko nkulondola. Ife tikukulandirani inu mu chiyanjano cha Mzimu Woyera.

<sup>234</sup> Ngati inu simunayambe mwabatizidwapo panobe, ndipo mukukhumba kuti mubatizidwe, yendani kubwera kuno ndi kudzawauza abusa za izo. Dziweli pano ngakhalenso liri ndi madzi mu ilo, usikuuno, ngati inu mukufuna kuti mubatizidwe. Chirichonse chiri mokonzeka. (Kodi inu munali nawo ubatizo, mulimonse? . . . ? . . .) Koma dziwe ndi lokonzeka, ngati aliyense akufuna kuti abatizidwe. Baibulo linati, “Lapani, aliyense

wa inu, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha tchimo lanu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezo liri kwa inu ndi ana anu, iwo omwe ali kutali komwe, onse omwe Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.”

<sup>235</sup> Inu mukumukonda Iye? Kwezani manja anu. [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] O, kodi Iye si wodabwitsa? Kodi inu mukusangalala nalo bwanji Bukhu ili la Ahebri? Inu mukulikonda Ilo? [“Ameni.”] Eya. Zodabwitsa. Tsopano, Ndi kukonza. O, Izo ndi zolimba ndipo Izo ndi zolunjika, koma ife tikuzikonda izo. Ndi momwe ife tikufunira kumakhala nazo Izo. Sitingakhoze kukhala nazo Izi mwa njira ina iliyonse.

<sup>236</sup> Tsopano, kodi inu mukukhulupirira kuti Paulo ali nawo ulamuliro woti azilalikira Izo monga choncho? Paulo anati, “Ngati Mngelo abwera ndi kudzalalikira uthenga wina uliwonse, musiyeni iye akhale wotembereredwa.” Kodi uko nkulondola? Chotero ife tikumukonda Iye ndi mtima wathu wonse.

<sup>237</sup> Tsopano ine ndikuti ndiwafunse abusa kuti abwere pano mphindi yokha, m’bale wathu wofunika kwambiri, M’bale Neville, ndipo iye akhala ndi mawu oti akuuzeni inu. Ndipo tsopano, ngati Ambuye alola, ife tidzakuwonani inu Lachitatu usiku, ndipo pangani zokonzekera kupita ku gulu la M’bale Graham Snelling ku kusionkhana kwa usiku. Ndiyenso kwa kulalikira kuno kuti tidzapitirize nazo, ndi mutu wa 7 ndi wa 8, Lachitatu usiku likubwera ili. M’bale Neville. 

*BUKHU LA AHEBRI*

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)